


AHEBRI, MUTU WACHINAI

 . . . ndi kuti tidziwe zochuluka za Ambuye athu odala. Ndipo ndicho—cholinga chatu chosonkhanirana muno, ndi kwa cholinga chimenecho, ndipo, tsopano, ndi kuwapempherera ana a Mulungu. Ndipo mmawawu ife tinali nalo—dalitso lodala kuchokera mu Malemba.

² Ife tikuyesera kuti titenge, nthawi iliyonse ya msonkhano, gawo la . . . ine ndikuphunzitsa mu Bukhu la Ahebri, takhala tiri, kwa masabata angapo apitawa tsopano. Ndipo tsopano, ngati Ambuye alola, ife tidzapitiriza Lachitatu usiku, kenako Lamlungu mmawa ndi Lamlungu usiku, p—pa, utali wonse womwe ine nditi ndikhale ndiri kuno mu nthawi iyi. Osati chitsitsimutso, koma ndi chitsitsimutso, msonkhano pa usiku wathu wachizolowezi. Ndipo kotero ife tiri kwambiri, okondwa kwambiri pokhala ndi nthawi iyi yoti tikomane ndi amzathu abwino ozungulira mu mizindayi, ndi ozungulira ku Mizinda ya ku Falls kuno. Ndipo ng—ngati ife tingapezeke kuti tiri ndi kusintha kapena chinachake, icho chingakhale kuti Ambuye akhoza kutitsogolera ife, posachedwapa, kuti . . . mwinamwake ife tikhoza kukhala ndi mausiku pang’ono, mwinamwake, mochitira masewero kapena chinachake, pakapita kanthawi, ngati Ambuye awoneka ngati akutitsogolera mwa njira imeneyo, kupita kumalo komwe ife tingakhoze kuwatengera anthu athu pamodzi.

Ndipo ife tinawaona anthu pamene ife timabwera kuno, akubwerera, akuti, “Munalibe malo k—kuti abwere mkati.” Chifukwa, kachisi ndi wamng’ono kwambiri. Iye amangokhalitsa, anthu apang’ono pang’ono kwambiri, ndipo ndife okondwa basi kuti inu mukulolera kubwera ndi kudzakhala mu kutentha, kuti mudzamve Mawu a Ambuye. Ndipo ife tikupemphera kuti Mulungu mopitirira muyezo, akudalitseni inu mochuluka ndi kukuthandizani inu.

³ Ndipo tsopano, usikuuno, ife tikufuna, ife tikuyambira pa mutu wa 4 . . . Ndi angati anali muno mmawawu? Tiyeni tiwone manja anu. O, ndizo zodabwitsa, mochitika nonse inu. Ndipo ife tiri pa, tikuyambira pa, mutu wa 4 wa Bukhu la Ahebri. O, Bukhu lonyumwitsa lakelo! Kodi inu mukukomedwa nalo Ilo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndipo iko ndi kufanizitsa Lemba ndi Lemba.

⁴ Ndipo Paulo, iye asanachitire konse umboni pa chomuchitikira chake, iye poyamba anayenera kuti apite ku Arabia ndi kukafufuza, mwa Mawu ngati izo zinali Choonadi. Ine ndikuzikonda zimenezo. Ndipo phunziro la mmawa uwu, ife tinapezamo uwu, mu kuphunzitsa mmawa uwu, kuti Khristu

anali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ndipo Paulo anapeza kuti Lawi la Moto lomwe lija limene linkawatsogolera ana a Israeli, linakomana naye iye pa njira yaku Damasko. Iye tinapeza kuti Lawi la Moto, lomwe linkatsogolera ana a Israeli kuchokera mu chipululu, kupita ku dziko lolonjezedwa, linakomana naye Paulo pa njira yaku Damasko, ndipo linadzitcha Lokha, “Yesu.”

⁵ Ndiye ife tikupezapo Umulungu wapamwamba weniweni wa Yesu Khristu. Bukhu lonseli apa ndi vumbulutso basi la Yesu Khristu. Ndipo Iye anabwera, ife tikupeza kuti, “Mu nthawi zamakedzana ndi mmanenedwe osiyanasiyana, Mulungu ankayankhula kwa makolo kupyolera mwa aneneri; mu masiku otsiriza ano kupyolera mwa Mwana Wake, Khristu Yesu.” Iye akudziulula Iyeyekha. Ndipo Bukhuli kuyambira ku Genesis mpaka ku Chivumbulutso si chinthu china koma vumbulutso limodzi lowirikiza, losalekeza, lopitirira, la Ambuye Yesu.

⁶ Ndipo ife tikupeza kuti Iye anali Yemwe anali mu chisamba choyaka. Iye tikupeza kuti Iye anali Yemwe anali ndi Mulungu asanaikidwe maziko a dziko. Ndipo ife tikupeza kuti, mu Chipangano Chatsopano, Iye anali Mulungu ndi Munthu, limodzi. Ndiyeno pamene Iye ankachoka mu Chipangano Chatsopano kuti apite Kumwamba, Iye anati, “Ine ndinabwera kuchokera kwa Mulungu, ndipo Ine ndikubwerera kwa Mulungu.”

⁷ Ndiyeno pamene Paulo anakomana naye Iye, Iye anali mu mawonekedwe omwewo amene Iye anali pamene Iye ankawatsogolera Aisraeli, Lawi la Moto. Ndipo Paulo anamuyang’ana Iye mu nkhope momwe, pokhala wosatembenuka, ndipo Izo zinamupangitsa iye kukhala ndi vuto la maso ake ena onse. Iye anapita ali wakhungu, ndipo kwa masiku angapo Iye sakanakhoza kuwona kanthu nkomwe. Iye anachita kutsogoleredwera ku msewu wotchedwa Wowongoka.

⁸ Ndipo Mulungu anali naye mneneri kumeneko yemwe Iye anayankhula naye, dzina lake Anania, yemwe anabwera uko, mwa masomphenya, ndipo anadzaika manja ake pa Paulo, ndipo anati, “M’bale Saulo, landira kupenya kwako.”

⁹ Ndipo ife tikupezapo, ndiye, kuti Mzimu Woyera womwe uja, Ambuye Yesu yemweyo, anabwera kwa Petro mu mawonekedwe a Kuwala ndipo kunamutulutsa iye mu ndende.

¹⁰ Ndipo ife tikupeza kuti Ambuye Yesu omwewo, mu masiku ano, akadali mu Lawi la Moto lomwelija (Kuwala) komwe kukuwatsogolera anthu Ake (Mpingo Wake), kumachita chinthu chomwecho, kupereka masomphenya; kubwera ndi kumaika manja pa anthu, mwa masomphenya. Ambuye Yesu, Yemwe ndinakomana naye Lamlungu lapitali mmawa kunyumba, ndipo anati, “Kunali bambo akubwera, wamutu wakuda, waimvi. Iye

anali wa Chigriki. Mkazi wake anali wa usinkhu wapakati, ndipo akanadzakhala akulira pa guwa.”

¹¹ Ena a iwo anali atawuzidwa icho, ndipo ankadziwa chomwe chinali kuchitika. Iye anali wolumala yense, m—msempha womuimitsa mmutu mwake unali utapita. Iye sankatha ngakhale kukhala ndi ulamuliro kwa mapazi ake kapena miyendo yake. Ndipo iye anali wakhungu. Ndipo kuti titsimikizire izo pawiri: ine ndinali ndi dona wamng’ono woti abwere kudzapempherera odwala, choyamba, ndiye ndinatembenuka apo ndi kuti M’bale Toms abwere kudzapemphera. Ndipo ife, titakhala apa, tikuziyang’ana izo zikuchitika. Ndiyeno ine ndinapita pansu ndi kukapempherera odwala, ndi kuyenda chobwerera. Ndipo iye anabwera, ndendende basi molingana ndi masomphenya, ndipo anandigwira ine pa nkono ndipo anayamba kulira, ndipo anati Dokotala Ackerman anali atawatumiza iwo kuno. Dokotala Ackerman ndi mzanga wapachifuwa wa ine, Mkatolika. Mnyamata wake ndi wansembe ku monastere k—ku Saint Meinrad, ndi uko mu Indiana. Ndipo bambo uyu anali wochokera ku Jasper. Ndipo Ambuye anamuchiza iye, kuchokera mu mpando umenewo. Iye anadzukapo ndipo anayenda. Iye anakhoza kupenya bwino monga wina aliyense. Ndipo anayenda natuluka mu nyumbayo, wabwino ndi wamphumphu. Zonse mwa masomphenya!

¹² “M’bale Saulo, Ambuye Yesu omwe anawonekera kwa inu muli panjira, andituma ine kuti ndidzaike manja anga pa inu, kuti inu mukhoze kulandira kupenya kwanu ndi kudzazidwa nao Mzimu Woyera.” Zodabwitsa.

¹³ “Ndiye ife tikupeza, powona kuti ife tiri ndi chipulumutso chachikulu ichi, ife tisamati. . . Ife sitikanakhoza kuthawa zilango ndi mkwiyo wa Mulungu, ngati ife tichinyalanyaza chipulumutso chachikulu choterechi.”

¹⁴ Tsopano ife tikuti tiyambe kuwerenga, usikuuno, kuchokera, ndipo tiyambira ndi mutu wa 4 Bukhu la Ahebri. Ngati aliyense akufuna kuti azitsatira limodzi, ife tiri ndi Mabaibulo ena pano. Ngati iwo akufunapo limodzi, mwakuti, mmodzi wa wothandizira abweretsa ilo kwa inu, ngati inu muti mukweze dzanja lanu, ma—Mabaibulo awa. Ngati mmodzi wa abale pano ati atenge. . . Pali Mabaibulo awiri ali apo, ine ndikukhulupirira.

¹⁵ Ndipo tsopano ife tifulumira, chifukwa ife tikhala ndi mgonero pakapita kanthawi. Ndipo pamene ife titi titsirizire usikuuno, Lachitatu usiku ife tidzayambira aponso. Tsopano, ine ndikukhulupirira, mmawa uno mu kuwerenga kwathu, ife tinayambira pa ndime ya 15.

¹⁶ Winawake, mwinamwake sakudziwa kuti ine ndikumavala magalasi, owerengera nao. Ine ndayamba kukalamba. Ndipo

ine ndikukhoza kumawerengabe, koma ine sindingakhoze kuzitenga izo mofulumira, makamaka pamene ine ndiri ndi zowerenga zazing'ono apa, zolemba zazing'ono.

¹⁷ Ndipo ine ndinapita kuti akandipime maso anga, kuti akawone ngati ine ndinalidi kutaya kupenya kwanga. Maso anga anali khumi pa khumi. Iye anati, “Koma iwe wadutsa makumi anai, mwananga.” Iye anali ndi chinthu choti ine ndizichiwerenga, anati, “Yamba kuwerenga chimenecho.” Ine ndinachiwerenga icho. Ndipo ine ndinayamba kuyandikirapo, izo zimayamba kuchedwera chedwera. Ndipo izo zinafika monga *chonchi*, ine ndimalekeza. Ndiye iye anaika apo pa khumi pa khumi, ine ndimakhoza kuwerenga izo paliponse. Koma iye anati, “Chomwe chiri, pamene iwe udutsa makumi anai, mipira ya mdiso lako imaphwa.”

¹⁸ Tsopano, ine ndikhoza kufinya maso anga ndi kuwerenga pafupi *chomwecho* basi kwa ine, koma iwe umayenera kuti ufinye. Chotero, iye anangondipangira ine magalasi. Ine ndikukhoza kumaziwona izo, paliponse, pamene izo ziri pafupi kwenikweni ndi ine. Tsopano, pamene izo zitalikira kwa ine, sindingakhoze kuwona konse ndi zinthu zimenezi. Koma ine ndimaziwerenga izo, kuwerenga kuchokera pa ichi ndi magalasi awa.

¹⁹ Tsopano, mmawa uno, ife tinali ndi gawo lotsiriza la mutu wa 3 wa Ahebri. Ndipo, o, zinthu zonona zomwe ife tinazipeza. Tsopano mvetserani. Ine ndikufuna kuti ndiziwerenge kachiwiri, chotero ife tipeze maziko tsopano. Osati kuyankhula pa izo, koma kukhala ngati kudutsa pa izo pang'ono.

Pamene zikunenedwa, Lero ngati inu...mumva liwu lake, musawumitse mitima yanu monga mwa kupalamula.

Pakuti ena, iwo, iwo anamva Mawu, pamene iwo anali atamva Mawu, anapalamula: ngakhale ziri choncho si onse omwe anachokera ku Igupto ndi Mose.

²⁰ Tsopano, mu izo, mmawa uno, ife tinapeza kuti Iye anati, “Musati muumitse mtima wanu tsopano, monga mu masiku a kupalamula.” Apo ndi pamene iwo anamupalamula Mulungu kuti akwiye, chifukwa kuti Iye anali atapereka kwa iwo Mose, mneneri Wake, ndi chizindikiro chomwe chinali ndi Mose. Ndi angati, a kalasi usikuuno, akudziwa chomwe chizindikiro icho chinali? Lawi la Moto, Ahebri 13.

²¹ Tsopano, ife sitikudziwa ngati osonkhana anachiwona chizindikiro icho kapena ayi. Koma Mose anachiwona Icho, pakuti Mose anakomana naye Iye poyamba mu chisamba choyaka. Iye anali Moto. Ndipo ana a Israeli anamumvera Mose, ndipo anachoka ku Igupto. Ndipo mwamsanga pamene iwo anatuluka ku Igupto, Mulungu, ife tikupeza, anawatsogolera

iwo ku msampha womwe. Kumene, ankhondo a Farao anali kumbuyo kwawo, Nyanja Yofiira kumbali inayo, ndipo Mulungu anawaika iwo pa yesero; ndipo iwo anachita mantha. Ndipo izo zinamupalamula Mulungu. Iye anati, “Chifukwa chiani iwe ukulirira kwa Ine?” Anati, “Ingoyankhula ndi kumapita patsogolo.” Ine ndikuzikonda zimenezo.

²² Tsopano, iwo anali kumutsatira Mose, pamene Mose ankatsatira Lawi ndi Mtambo, ndipo iwo anali panjira yawo waku dziko lolonjezedwa. Chithunzi chokongola cha Mpingo, usikuuno, paulendo wathu waku Dziko lolonjezedwa, tikutsogozedwa ndi Mzimu womwewo, zizindikiro zomwezo ndi zodabwitsa momwe Mulungu anayankhulira pa izo.

²³ Tsopano zindikirani. Ndiye, iwo anafika ku Chipululu cha Sini. M—madzi anali “owawa,” *Marah*. Nchifukwa chiani Mulungu anawatsogolera iwo ku madzi owawa? Zikuwoneka ngati Iye akanawatsogolera iwo ku madzi abwino. Koma Iye anawatsogolera iwo ku madzi owawa chotero kuti Iye akanakhoza kutsimikizira chikhulupiriro chawo. Iye amakonda kuchita zimenezo. Iye amakonda kulola zisautso zibwere pa iwe, kusonyeza kuti Iye akhoza kukusonyezani inu chikondi Chake ndi mphamvu Yake. Anthu angathe bwanji, lero, omwe samakhulupirira mwa Mulungu wochita zozizwitsa. . . Pamene masautso abwera, iwo amangosiya ndi kumapitirira. Koma ife tikukhulupirira kuti “Mulungu amachita zozizwitsa.” Iye sangati. . . Mulungu ali. . .

²⁴ Mvetserani kwa izi. Ngati Mulungu sangachite mofanana, pamene zochitika zomwezo ziwuka, ndiye Mulungu ali wolakwa pa kukhala wokondera kwa anthu Ake. Kuchita mwayekha kwa Mulungu kumamukakamiza kuti Iye azigwira ntchito mu vuto lirilonse momwe Iye anachitira pa vuto loyamba, kapena Iye analakwitsa pamene Iye anachita mu vuto loyambalo. Ngati Mulungu sangati achite mwa njira yomweyo Iye anachitira pa vuto loyamba, ngati Iye ati achite mosiyana kwa vuto lachiwiri, ndiye Iye anachita molakwitsa pamene Iye anachita pa vuto loyambalo. Ngati Mulungu ankachiza wodwala mu Chipangano Chakale, Iye ayenera kuti azichita izo mu Chipangano Chatsopano ndi lero, kapena Iye anachita molakwitsa pamene Iye anawachiza iwo kumbuyo uko. Iye ayenera kumachita mofanana, nthawi iliyonse. Ndipo Iye azichita izo, pamene chikhulupiriro chomwecho chikomana ndi zofunikirazo. Kulephera kuli mwa ife, osati mwa Mulungu. Pakuti ife tikumuwona Iye pa ena, ndi ochuluka, akuchita zozizwitsa zazikulu zowoneka. Ife tikudziwa zimenezo. Wotsutsa sangati, “Siziri chomwecho.” Pakuti ife tikuziwona Izo zikutsimikizira izo, ndipo apo izo ziri.

²⁵ Iwo anakonda kumati, “Ndisonyeze ine chozizwitsa.” Iwo sangathe kunena izo panonso. Sayansi singakhoze kunena izo panonso. Ife tikhoza mwamtheradi kutsimikizira kwa dziko

lasayansi. Ndipo dziko lasayansi lachitira umboni kuti Chinthu chazimu, mwa mawonekedwe a Lawi la Moto, chiri ndi ife. Chithunzi Chake ndi ichi apa, pano pomwe, ndipo chimodzi chapachikidwa mu Washington D.C., usikuuno. Uyo ndi Khristu yemweyo.

²⁶ Chotero, mwa kanthawi, abale anga otumikira anakonda kumandiuza ine, “O, M’bale Branham, ameneyo ndi Mdierekezi. Musati mudzipusitse ndi izo.” Anali kundiwopsyeza ine.

²⁷ Ndipo ine sindikanalalikira izo mpaka Mulungu anabwera ndipo anaziulula izo, kuti, “Iye ali Yesu yemweyo, Mmodzi yemweyo.” O, ndiye muyesere kuti muzigwedeze izo mozichotsa kwa ine? Sizingachitike. Pakuti, ndi Lemba. Ndi Mawu a Mulungu. Si chongondichitikira chomwe chiri chawamba. Ndi chondichitikira chomwe chaimiridwa kumbuyo ndi Mawu a Mulungu ndi lonjezo lodala Lamuyaya la Mulungu.

²⁸ Tsopano, ife tikuzindikira cha apa, ndiye, kuti Iye anati.

Pakuti ena, pamene iwo anamva, anapalamula: . . .

Ndithudi. Iwo anayamba kutopa, nthawi iliyonse iwo akafika pa malo pomwe chiwonetsero chimabwera. Ndiye kodi iwo amachita chiani? Iwo amakhoza kunyanyukapo, ndi kuyamba kutopa, ndi kumafuna kuti abwerere mmbuyo, ndi, “Chifukwa chiani izi zandichitikira ine?”

²⁹ Chinthu chachilendo, mmawa uja, nditatha kulalikira izo zolimba basi momwe ine ndikanathera, apo panali ambiri omwe anabwera kuguwa ndipo amafunsa Izo, “Chifukwa chiani izi zikuchitika kwa ine?” Inu mukuwona momwe Izo zimayendera? Izo zimapita pamwamba pa mitu ya anthu. Ndi zofanana basi, anthu.

³⁰ Yesu anati, “Inu muli nawo maso, koma inu simukutha kupenya.” Iye ananena zimenezo kwa ophunzira.

³¹ Iwo anati, “Taonani, tsopano Inu mukuyankhula mwachimvekere. Tsopano ife tikukhulupirira. Palibe munthu angati azikuwuzani Inu chirichonse, chifukwa Mulungu amawonetsa izo kwa Inu.”

³² Iye anati, “Kodi inu mukukhulupirira tsopano, itatha nthawi yonse iyi?” Mukuona?

³³ Inu musamakhalé ndi funso pa chirichonse, kwa Mulungu. “Pakuti mapazi a olungama amatsogozedwa ndi Ambuye.” Ndipo yesero lililonse limaikidwa pa inu, kuti litsimikizire inu. Ndipo Baibulo linati, “Iwo ndi ofunikira kwambiri kwa inu kuposa golide.” Chotero ngati Mulungu alola mazunzo opepuka pang’ono achitike kwa inu, kumbukirani, izo ndi zoti zikukonzeni inu. “Mwana aliyense yemwe abwera kwa Mulungu ayenera poyamba kuti akwapulidwe ndi Mulungu, ndi kuyesedwa, kuphunzitsa mwana.” Palibe kupatula. “Mwana aliyense yemwe abwera.” Masautso awo amachitidwa kapena

akubweretsedwa—amabweretsedwa apo, kuti awone momwe inu muti muzitengere izo. Mukuona? Ndi Mulungu, pa bwalo lotsimikizira ili. Ndizo zonse dziko lapansi liri, ndi mabwalo otsimikiziramo, ndi kumene Iye akuyesera kuti atsimikizire inu.

³⁴ Tsopano mvetserani, pamene ife tikupitirira. Ndipo ine ndikufuna kuti nditenge gawo lotsiriza la izi.

Ndi kwa yemwe iye analumbira kuti asakalowe mu mpumulo wake, . . .

Tsopano, apo ndi pamene ife tikubwerapo, usikuuno.

. . . mu mpumulo wake, koma kwa iwo omwe sanakhulupirire?

Kotero ife tikuwona kuti iwo sakanakhoza kulowa . . . chifukwa cha kusakhulupirira.

³⁵ Tsopano, kodi tchimo ndi chiani? Kusakhulupirira. Mulungu ankabwera kwa iwo, mu Lawi la Moto; anatumiza mneneri Wake, ndipo anamudzoza iye, anamupatsa iye zizindikiro zoti azikachita pamaso pa anthu. Ndiyeno Lawi la Moto, mwa mneneri, linkawatsogolera iwo potuluka. Chochitika chirichonse chomwe iwo ankafikapo, iwo ankayamba kung'ung'uza ndi kumanena vuto laling'ono lililonse lomwe iwo ankalipeza ndi Mose, anayamba kulalata ndi kuyankhula momutsutsa Iye. Ndipo Mulungu sizinamusangalatse, chifukwa Iye anati, “Iwo anali kuchimwa.”

³⁶ Iwo akanati azimvetsera. Koma, mmalo mwa izo, iwo ankamvetsera ku kulingalira, “Izo zingakhale bwanji? Zinthu izi zingakhale motani?” Ngati Iye ali Mulungu, chirichonse ndi chotheke. Ndipo Iye apanga zinthu zonse kugwirira ntchito limodzi kwa ubwino wa iwo omwe akumukonda Iye.

³⁷ Tsopano ife tikupita mu kuphunzira kwakukulu apa, uko ndiko, pa “Mpumulo,” *sabata*. Tsopano, iwo anali amwendamnjira mu ulendo wawo. Mukuona? Iwo anali ali uko mu Igupto, zaka mazana anai, ndipo mu nsinga. Ndipo tsopano iwo anali akutulutsidwa mwa zozizwitsa za Mulungu, molingana ndi lonjezo Lake. Ndipo iwo anali pa njira yawo waku dziko lolonjezedwa. Ndipo apa Kuwala kwauzimu kunawonekera, pakati pa iwo, ndipo kunayamba kuwatsogolera iwo.

³⁸ Tsopano, winawake akanati, “Tsopano, yang'anani apa, kodi Mose uyu ndi ndani? Nndani anakupanga iwe wolamulira pa ife? Kodi iwe si mmodzi wa ife? Ndani anakuika iwe apa kuno kuti ukhale bwana wathu? Iwe ukuganiza kuti iwe ukudziwa mochuluka kuposa momwe abusa athu amachitira? Iwe ukuganiza kuti ukudziwa kuposa momwe ansembe athu amachitira? Iwe ukuganiza kuti n—ndiwe wanzeru kuposa chomwe amuna athu achipembedzo ali, a tsiku lino?” Izo zinalibe chinthu chochita ndi izo.

Uyo anali Mulungu, mu Lawi la Moto, akutsimikizira kuti Iye anali mu kuyendako. Izo sizinkapanga kusiyanana kulikonse yemwe anali wanzeru ndi yemwe sanali wanzeru. Ilo linali lingaliro la kutsatira chomwe Mulungu anachiika patsogolo pa iwo.

³⁹ Pakuti, Mose, tikanena mwathupi, anachita chinthu chopusa pamene iye ankayesera kuti awatulutse ana mwa Mawu a Mulungu, kutengera gulu la anthu kupita mu chipululu. Pamene iye anali nawo ake. . . Pakuti, iye anali wolandira kwa chirichonse chomwe iwo anali nacho. Iye anali nawo ankondo aliwonse omwe analipo, mu dziko lonse, atakwapulidwa. Ndipo apo iye anali, mtsogoleri wamkulu wankhondo. Ndipo kusuntha kotsatira, iye anali woti akhale mfumu, Farao waku Igupto. Bwanji, iye akanangodzakhala pa mpandowachifumuwo, ndipo nati, “Chabwino, ananu, zibwereranino kwanu.” Izo zikanakhazikitsa izo; iye anali Farao. Koma Mose. . .

⁴⁰ O, ndi izi apa. Mose, mwa *chikhulupiriro*, analiwona lonjezo la Mulungu. Ndipo Mngelo wa Ambuye anadza kwa iye, ndipo iye anadziwa mochulukwa za Mulungu, mu maminiti asanu mu Kukhalapo kwa Mngelo ameneyo, kuposa zomwe iye anaziphunzira mu zaka makumi anai ndi aphunzitsi aku Igupto. Iye anadziwa kuti Iye anali. Iye anawona chazimu chikuchitidwa.

⁴¹ Iye anati, “Ine ndikhala ndiri ndi iwe, Mose. Ine ndizipita patsogolo pako.” Ndipo iwo anamvetse. Ndipo Iye anamupatsa iye zizindikiro zoti azizichita.

⁴² Tsopano, iwo anali ali panjira yawo waku dziko la mpumulo. Mulungu anali nawo kwa iwo mpumulo, malo omwe iwo sakanati akakhale aku. . . mabwana pa iwo, kuti aziwawongolera iwo, kuti aziwapangitsa iwo kuchita zinthu.

⁴³ Chithunzi chake chokongola chomwe icho chiri lero, pamene ife tikuyang’ana pa Mpingo ndi kuwona Mpingo mu chikhaliidwe chake, munthu aliyense yemwe ali wobadwa mwa Mzimu wa Mulungu amalinyoza dziko. “Ndipo ngati inu mukonda dziko kapena zinthu za mdziko, chikondi cha Mulungu sichiri nkomwe mwa inu.” Ndi zomwe Baibulo linanena. Ndipo mwendamnjira weniweni, pa ulendo wake, mophweka amazida zinthu za mdziko. Iye amadana nazo kumuwona mwamuna akumwa. Iye amadana nazo kumuwona mwamuna akusuta. Iye amadana nazo kuwaona akazi pa msewu, atavala tizovala tonyansa tating’ono ito. Iye amadana nazo kuwona zisudzo ndi maphwando a njuga.

⁴⁴ Ndipo dzulo, pamene M’bale Tony. . . kapena M’bale Woods ndi ine tinali kubwera podutsa mu msewu, ndi ena ochulukwa, ena a amuna. . . Apo panali dona wamng’ono apo mu Louisville, akubwera motsika ndi msewu, mkazi wamng’ono wowoneka mokondeka, atavala zovala zomwe zinali zoipa; ziri basi mmwamba momwe mchiuno, ndi kaduwa

kakang'ono katamangidwa mchiuno mwake, kumbali iliyonse, ndi kachidutswa kakang'ono ka nsalu kozungulira kutsogolo kwake, ndipo atakamanga ndi kachingwe kumbuyo. Akuyenda ndi msewuwo, moipa, ndipo munthu aliyense pa msewu akumuyang'ana iye. Ine ndinati, "Iye sakuzindikira kuti iye ndi wolakwa, pamaso pa Mulungu, pakuchita chigololo ndi mwamuna aliyense yemwe akuyang'ana pa iye mu chikhalidwe chimenecho. Ndipo iye adzakayankha pa tsiku lachiweruzo pa kuchita chigololo ndi amuna amenewo."

⁴⁵ Yesu anati, "Aliyense yemwe ayang'ana pa mkazi mpaka kumukumbira iye, wachita kale chigololo ndi iye." Ndiko kulondola.

⁴⁶ Chotero, inu mukuona, M'bale Woods anati kwa ine, "Mungaloleze chiani pa izo, M'bale Branham?"

⁴⁷ Ine ndinati, "Izo mwina ndi kuperewera kwa ubongo kapena kugwidwa ndi ziwanda." Pali zinthu ziwiri zokha zoti zingapange izo. Mkazi wakhalidwe, wabwino bwino sangavale zinthu zimenezo; kupatula ngati iye atakhala wogwidwa ndi ziwanda. Ndizo ndendende Choonadi.

⁴⁸ Tsopano, mwendamnjira yemwe ali paulendo wake wa Kumwamba, iye amakhala mu chikhalidwe chosiyana. Inu simumasowa kuti muzidandaula za iye kuti ayang'ana pa iye. Iye apotoloza mutu wake ngati iye ali naye Mulungu mu mtima mwake, pakuti iye akukhala mu chikhalidwe chomwe chiri mamailosi milioni kuchokera ku zinthu zimenezo. Ndiko kulondola. Iwe sukufuna kuti udzakhale wolakwa ndi zinthu zimenezo, pa chiweruzo. Chotero iye amapotoloza mutu wake nkuti, "Mulungu, muchitireni chifundo mkaziyo," ndipo mopitirira iye amapita. Iye tiri mu ulendo wathu. Iye tiri pa ulendo wathu waku Dziko la Kenani. Iye tiri pa njira yathu ku Mpumulo Wamuyaya uwo ndi wamadalitso umene Mulungu watipatsa ife. Ndipo mu ulendowu, ife timayesedwa. Iye timayesedwa ndi mitundu yonse ya zinthu, komabe nkukhala tikuyesedwa wopanda kumachimwa.

⁴⁹ Tsopano zindikirani, pamene ife tikupita ku mutu wa 4, "Tiyeni ife chotero tiwope."

Tiyeni ife chotero tiwope, mwina, lonjezo lingatisiye ife kuti tilowe mu mpumulo wake, . . .

⁵⁰ Ine ndikufuna inu kuti mukumbukire, kuti, kupatula ngati ife tingafufuze, kupatula ngati Mulungu ataululira izo kwa ife! Ziribe kanthu mochuluka kwa momwe ife timapitira ku tchalitchi, izo ziribe kanthu kochita ndi izo. Mulungu ayenera kubwera mwa vumbulutso ndi kudzadzululira Iyeyekha kwa ife, izo zimatengera zinthu zonse za mdziko kunjira. "Tsopano, pamene ilo likutchedwa, 'Lero ngati inu . . .'"

⁵¹ Tsopano tiyeni tiyambire—mutu wa 4.

Tiyeni ife chotero tiwope, mwina, lonjezo lingatisiye ife kuti tilowe mu mpumulo wake, . . .

52 Tsopano kumbukirani, pamene iwo anali pa ulendo wa ku Mpumulo, Lawi la Moto linkawatsogolera iwo. Tsopano ife tikufuna kuti tipeze, “Kodi Mpumulo uwu ndi chiani?”

Tiyeni ife. . . tiwope, mwina, lonjezo lingatisiye ife kuti tilowe mu mpumulo wake, penyani, aliyense wa inu angakhale ngati akuperevera kwa ilo.

53 Tsopano, apa pali lonjezo. Apa pali chimene ife tiyenera kuti tichiwope: ngati palibe lonjezo latisiya ife. Koma pali lonjezo! Ndiyeno, chinthu chotsatira, musati muperevera kwa ilo.

54 Tsopano, lingaliroli ndi lakuti, ngati ife tiri pa njira yathu kupita ku Mpumulo, kodi Mpumulo ndi chiani? Kodi iwo uli kuti? Kodi iwo ndi kujowina mpingo? Kodi iwo ndi kubatizidwa mwanjira inayake? Kodi ndi kukhala membala wa mpingo waukulu kwambiri mu mzinda? Kuvala zovala zabwinoko? Kodi ndi maphunziro? Kodi ndi ndalama, koto ife tikhoza kusiya ntchito ndi kumangokhala, kupumula mpumulo wa moyo wathu, monga ife timazitchela izo? Sindizo izo ayi.

55 Mvetserani zomwe Baibulo limanena kuti iwo uli, ndi momwe ife timaopezera iwo.

Tiyeni ife chotero tiwope, mwina, lonjezo linatisiye ife kuti tilowe mu mpumulo wake, aliyense wa inu angaoneke ngati akuperevera kwa ilo.

Pakuti kwa ife (tsikulo ndiye) uthenga unalalikidwa, chimodzimodzinso ndi kwa iwo: . . .

Uthenga ndi chiani? Nkhani yabwino. Nkhani yabwino inabwera kwa iwo mu Igupto, kuti, “Mulungu watumiza muwomboli, ndipo Iye atitulutsa ife ndi kutitengera ife ku dziko lamalonjezo.”

56 Nkhani yabwino kwa ife tsopano, ndi yoti, “Mulungu watumiza Muwomboli, Mzimu Woyera, ndipo ife tiri panjira waku Dziko lamalonjezo.” Tsopano anthu alipanga ilo tizikhulupiriro ndi zipembedzo, koma Mulungu akukhalabe, kuti, *Mpumulo* wathu ndiwo “Mzimu Woyera.”

57 Zindikirani.

. . . uthenga unalalikidwa . . . kwa iwo chimodzimodzinso ndi kwa ife: koma mawu omwe analalikidwa sanawapindulire iwo, a . . .

Kumbukirani:

. . . mawu analalikidwawo sanawapindulire iwo, posakanizidwa ndi chikhulupiriro mwa iwo omwe anawamva iwo.

58 O, abale anga, ndiroleni ine ndiime apa kwa miniti. Ziribe kanthu momwe Mawu alalikidwira mochuluka,

mwabwino momwe inu mukuwakondera momwe Iwo akhala ali kulalikiidwira; kupatula ngati inu enianu muli ogawana nawo Iwo, Iwo sati akuchitireni inu chidutswa chimodzi cha ubwino.

. . . pokhala asanasakanizidwe ndi chikhulupiriro ndi iwo omwe anawamva iwo.

⁵⁹ Iwo anawona zozizwitsa za Mose. Iwo anati, “Izo ndi zabwino kwambiri.” Ndipo iwo anayenda napitako. Iwo, iwo anamuwona iye akuchita zozizwitsa. Ndipo iwo anawona Lawi la Moto, mwinamwake, kapena anawamva iwo akuyankhula za Ilo. “O, izo zonse nzabwino.”

⁶⁰ Koma izo sizinasakanizidwe ndi chikhulupiriro chapayekha. Pakuti mwamsanga pamene iwo anafika ku chipululu, iwo (aliyense) anayamba kung’ung’uza. Ndipo Mulungu anati, “Chifukwa kuti iwo akaikira, ilo linali tchimo.” Musati muzikaikira kanthu kena. Zikhulupirirani. Musati muzikaikira, ziribe kanthu momwe vutolo liri lolimba, ziwakhulupirirani Iwo.

⁶¹ Tsopano iwo anayamba kung’ung’uza, ndipo Mulungu anawagonjetsa iwo. Ndiyeno Iye analumbira, mu mkwiyo Wake, kuti, “Iwo sadzalowa konse mu Mpumulo Wake.” Ndipo Baibulo linanena apa, ine ndikukhulupirira Izo ziri mu—mutu wa 3, kuti, “Matupi awo anagwera mu chipululu.”

⁶² Mutu wa 3 ndi ndime ya 17.

Koma omwe iye anakwiyyitsidwa nawo kwa zaka makumi anai? Kodi sizinali ndi iwo omwe anali atachimwa, omwe matupi awo anagwera mu chipululu?

⁶³ Ndipo mwa onse awo omwe anabwera kuchokera ku Igupto, awiri okha anapita mu dziko lamalonjezo. Kuchokera mu dziko lonse la chigumula, mu masiku omwe anapitawo, uko kunali miyoyo isanu ndi itatu inapulumutsidwa, kuchokera mu mabilioni. “Khwala ndiro chipata ndipo njirayo ndi yopapatiza, ndipo koma apang’ono adzakhalapo omwe ati adzaipeze iyo.”

⁶⁴ Anthu ena amati, “Ndiye, M’bale Branham, nanga bwanji zikwi zonse zija zomwe Baibulo limati zidzakawonekera kumeneko?”

Ingokumbukirani ndi angati afa mu kam’badwo kalikonse, omwe akhala ali Akhristu, mmusimo kudutsa mu m’badwo. Iwo onsewo adzauka. Awo akupanga Thupilo. Inu mukuyembekeza kuti padzakhale bilioni zana mu Amereka uyu, ati adzatulukemo, kapena ena ake, dziko ili lero. Mwina sipadzakhoza kukhala makumi asanu ati adzatulukemo. Koma Mpingo wawukulu wowomboledwa uli mu fumbi, ukuyembekeza. Iwowo ndi ngale za Mulungu zomwe zikupuma mu fumbi. Koma miyoyo yawo ili pansi pa guwa la Mulungu.

Iwo sali mu chikhalidwe chawo choyenera. Iwo ali mu thupi, moonadi, koma la fiofane. Ndipo iwo akumafuulira kwa Mulungu, “Mpaka liti?” Iwo akumakhoza kuwonana wina ndi mzake, koma iwo sangakhoze kugwirana chanza wina ndi mzake, thupi la mtundu umenewo.

⁶⁵ Inu mukanakomana nawo amayi anu mu Ulemerero usikuuno, ngati inu mungati mupite, inu simukati mugwirane nawo chanza chifukwa alibe dzanja la mtundu umenewo. Inu simukanakhoza kumverera izo monga inu mungamamverere pano. Chifukwa, zokhudzira zisanu ndi zomwe zaikidwa mu thupi ili, zomwe zizilamulira. Kukhalapo kwa izo kukamakhoza kumakamvereredwa mu chikhalidwe chosiyana.

⁶⁶ Ndizo monga mwamuna ndi mkazake. Uko sikukakhala kukwatira, kapena kuperekedwa mu chikwati, Kumwamba. Bwanji? Chifukwa uko kuli mtundu wosiyana wa chikondi. Uko kulibe chikhumbo chakugonana. Zinthu zonse izo zapita kutali. Inu mwatsukidwa ndinu angwiro.

Koma inu simunayambe mwakhalapo mu chikhalidwe chimenecho, chotero inu simunalengedwere chikhalidwe chimenecho. Inu mukungoyembekezera kumeneko. Koma inu mukukhumba kuti mubwererensu komwe inu munalengedwa mwamuna ndi mkazi, ndipo uko Mulungu adzaliukitsa thupi limenelo kuchokera ku fumbi la dziko lapansi ndi kulipatsa ilo ulemerero. Ndiyeno inu muzidzapenya, kulawa, kumverera, kununkhiza ndi kumva, ndi kuyanjana. Ife sitidzadziwa konse...

Ife sitingakhoze kusangalala nao moyo wa Mngelo. Ife sitinalengedwe kuti tikhale Angelo. Mulungu anawalenga Angelo. Koma Iye anakulengani inu ndi ine, amuna ndi akazi. Ndicho chikhalidwe chomwe ife titi tidzakakhalemo, kwanthawizonse, pa Kudza Kwake kodala.

⁶⁷ Tsopano, onani momwe iwo anaperewerera, chifukwa iwo anachimwa ndipo anaperewera kwa ulemerero. Mulungu anawasonyeza iwo Lawi la Moto. Iye anawasonyeza iwo zizindikiro ndi zodabwitsa. Iye anawatsogolera iwo atuluke. Iye anawabweretsa iwo ku kuyesedwa, kuti awayese ndi kuwatsimikizira iwo.

⁶⁸ Tsopano, kodi simunakhale nawo mayesero ochuluka? Musati muzidandaula za iwo. Zisangalalani. Mulungu ali nanu. Iye akuyesera kuti atsimikizire chikhulupiriro chanu. Yang’anani pa Yobu mu Chipangano Chakale, pamene Iye anati, “Kodi iwe wamulingalira wantchito Wanga Yobu, mwamuna wolungama, mwamuna wangwiro? Palibe wina wonga iye pa dziko lapansi.”

⁶⁹ “O,” iye anati, “zedi, Inu mwamutchingira iye: samakhala ndi mavuto aliwonse, samakhala ndi kudandaula kulikonse. Iye samakhala ndi kulemedwa kwa zachuma kulikonse, chirichonse

chiri bwino. Iye samakhala ndi matenda aliwonse, kuwawa kulikonse. Ndiroleni ine ndikhale naye iye. Ine ndimupangitsa iye kuti akutukwaneni Inu, pa nkhope Yanu.”

⁷⁰ Iye anati, “Iye ali mdzanja lako, koma usati utenge moyo wake.”

⁷¹ O! Iye anachita chirichonse kupatula kutenga moyo wake, koma iye sanathe kumusuntha Yobu. Yobu ankadziwa kuti iye anaima njii pa Mawu. Ndiko kulondola. Ndipo adierekezi onse ochokera ku hade sakanakhoza kumusuntha iye, pakuti iye ankadziwa kuti iye anali atapereka nsembe ija. Iye anali wolungama. Ndipo iwo anamutsutsa iye, anati, “Iwe wachimwa, Yobu, ndipo Mulungu akukulanga iwe.” Iye ankadziwa kuti Mulungu sanatero...kuti iye anali asanachimwe pamaso pa Mulungu. Iye ankadziwa kuti iye anali wolungama. Osati chifukwa chakuti iye anali munthu wabwino, koma chifukwa Iye anali kulandira nsembe yopyereza mmalo mwake.

⁷² Ndipo, usikuuno, ife tikudziwa kuti moyo wake unatsimikizira kuti iye anali wolungama. Ndipo pamene inu... Osati kuyesera kuti mukafike kwathu ku Ulemerero chifukwa choti inu mumayesera kuwathandiza oyandikana nawo anu; izo ndi zabwino. Osati chifukwa chakuti inu munajowina mpingo; izo ndi zabwino. Koma inu mukafika kwanu ku Ulemerero chifukwa inu munavomereza chilungamo cha Yesu Khristu, palibe kanthu komwe inu mwachitapo inueni.

⁷³ Tsopano, pamene ife tikuweranga mopitirira.

Pakuti kwa ife uthenga unalalikidwa,...(ndime ya 2)...chimodzimodzi monga kwa iwo: koma mawu omwe analalikidwa sanawapindulire iwo, posakanizidwa ndi chikhulupiriro mwa iwo omwe anawamva iwo.

Chikhulupiriro munalibe mwa iwo omwe anawamva Mawuwo.

⁷⁴ Tangoganizani, lero, mu utumiki waung’ono, wonyozeka umene Ambuye andipatsa ine, kunayenera kukhala kuli Achimereka mamilioni makumi anai atapulumutsidwa, usikuuno. Inu mukudziwa zomwe iwo amanena? “Bwanji, uwo ndi m’bwebwe wa maganizo. Iye ndi wowerenga malingaliro. Palibe zinthu zoterozo! Bwanji, iye si wa mu mpingo wathu.” Mukuona? Sindizo...ziribe kanthu momwe iwe ukuyalira mochuluka pa Mawu ndi kutsimikizira kuti ndi Mawu a Mulungu, ndi lonjezo la Mulungu, mochuluka sayansi ingatsimikizire kuti Izo ndi zoono, iwo apobe sangakhoze kuzikhulupiririra. Baibulo linati iwo sakanakhoza.

⁷⁵ Mukuti, “Ndiye ndi za ntchito yanji kuwalalikirira Iwo?” Mulungu ayenera kuti adzakhale ndi mboni, kuti idzawatsutse iwo, pa Tsiku limenelo. Mawu alalikidwa ndipo atsimikiziridwa pakati pawo, ndipo iwo apabe mwaumbuli akumayenda

nachokapo. Palibe china chatsalira koma chiweruzo. Mulungu sangakhoze molungama—sangakhoze molungama kuliweruza fuko kupatula ngati ilo likanakhala ndi chifundo ilo lisanakhale ndi chiweruzo. Iye ndi Mulungu. Iye sakanakhoza kuchita zimenezo.

⁷⁶ Tsopano kodi ife tikuti chiani?

Pakuti ife amene . . . takhulupirira nafenso talowa mu mpumulo, monga iye anati, Monga Ine ndalumbira mu mkwiyo wanga, ngati iwo ati adzalowe mu mpumulo wanga: ngakhale ntchito zinali zitatsirizidwa kuyambira ku maziko a dziko.

Pakuti iye anayankhula mu malo ena p—pa tsiku lachisanu ndi chiwiri motere, . . .

⁷⁷ Tsopano, ine sindikufuna kuti ndipweteke kumverera kwa anthu, motsutsana ndi chipembedzo chawo. Icho si cholinga changa. Kunja ku mindako, ine ndimangolalikira ziphunzitso zachizolowezi, zaulaliki, zachikhazikitso. Koma mu kachisi, pakati pa ana anga pano, ine ndikumverera kuti ine ndiri nawo ufulu woti ndizilalikira chomwe ine ndikuganiza kuti ndi Chiphunzitso ndi Choonadi. Mukuona? Ine ndikuganiza kuti icho ndi cholondola.

⁷⁸ Tsopano, ine ndiri nawo zikwi za abwenzi abwino Achi Sabata, anthu omwe ali a Seventh-day Adventist. Ena a abwenzi okonedwa kwambiri omwe ine ndiri nawo, ena a iwo ndi a Seventh-day Adventist.

Ngakhale, kusuntha kwakukulu kwa, zomwe zimatchedwa, 1—*Liwu la Uneneri*, iwo amatsutsana ndi ine molimba. Iwo amanena kuti ine ndimapanga maneno paguwa, ndi kuti, “Ine ndi Mulungu. Ndi k. . . ndi kuti Kuwala uku kumene kumanditsatiraku ndi Mngelo, ndipo ine ndi Mulungu. Ndipo ine ndinabwera ku dziko kuti ndidzachite zinthu zazikulu, kuti ndidzatsimikizire kwa anthu kuti ine ndine Mulungu.” Tsopano, ndizo zomwe a *Liwu la Uneneri* amanena zokhudza ine, uko ku California. Ndipo aliyense yemwe anawauza zimenezo, inu mukudziwa, anawauza chinachake chomwe sichinali chomwecho.

⁷⁹ Koma mu malo oyamba, osati kutengapo lingaliro mowatsutsa a mpingo wa Seventh-day Adventist kapena mpingo wina uliwonse Wachi Sabata, koma kokha chifukwa cha Uthenga. Ife tifika pamenepo, mu maminiti pang’ono, pa Achipentekoste, nawonso. Eya. Pa Abaptisti, ife tifika mpaka pa zimenezo ndi kusonyeza kuti Mulungu samakondera chipembedzo chirichonse. Ndiko kulondola. Iye amangokondera munthu payekha. Ndipo Iye samachita ndi chipembedzo chirichonse, Iye sanayambe wateropo ndipo Iye sadzatero nkomwe, malingana ndi Mawu Ake. Koma Iye amachita ndi

munthu payekha mu chipembedzo chirichonse. Inde, ndi munthu payekha yemwe Mulungu amachita naye.

⁸⁰ Tsopano mvetserani kwa izi momveka kwenikweni, ndipo ngati konse, nthawi iliyonse, funso limenelo liti lidzabwere konse kwa inu, ilo lidzakhala litathetsedwa. Tsopano, Ambuye atatithandiza ife.

⁸¹ Tsopano, mwatcheru, “Pakuti . . .” Ndime ya 4.

Pakuti iye anayankhula mu malo ena za tsiku lachisanu ndi chiwiri motere, . . .

⁸² Tsopano penyani. Iye akuyankhula za sabata. Ndi angati akudziwa kuti mawu okuti *s-a-b-a-t-a* mu Chiheb- . . . ndi mawu Achihebri omwe amatanthauza “m-p-u-m-u-l-o”? Ndi angati amadziwa zimenezo, mu Chichewa? Zedi. Kodi *sabata* silimamveka ngati mawu achilendo? Iwo ali.

⁸³ Kodi *sanctify* samamveka ngati ndi mawu achilendo? *Sanctify* ndi mawu Achigriki. *Sanctify* amatanthauza “kupangidwa woyera.” M’chihebri, amatanthauza “kupangidwa woyera.” M’chigriki, amatanthauza “kuyetsa.” Mchingerezi, amatanthauza “kupangidwa waukhondo.”

⁸⁴ *Sabata* imatanthauza “tsiku la mpumulo.” Ndicho chomwe sabata yakale inali, tsiku la mpumulo. Pamene inu muwona *mpumulo*, iwo ukutanthauza “sabata.” Kayang’anani izo mu zolemba zanu zapachiyambi, ngati mupezeka kuti muli ndi Baibulo Lachigriki, ndi kukafufuza ngati mawuwu . . . Ngati inu muli ndi Baibulo la Scofield, yang’anani mu zowerenga zanu za mmphepete pa “mpumulo” ndi kuwona ngati izo sizikukubweretsani inu mmbuyo ku *sabata*. *Sabata* imatanthauza “mpumulo.” Chabwino.

⁸⁵ Tsopano penyani.

Tiyeni ife chotero tiwope, mwina, lonjezo likhala litasiyidwa kwa ife loti tilowe mu sabata lake, mpumulo, . . .

⁸⁶ Tsopano, anthu ambiri amasunga masiku, monga kusunga tsiku la sabata *Loweruka*. Ena amalipanga *Lamlungu* fano, tsiku lopembedza. Ndipo mwa chisomo cha Mulungu, ndi mwa Mawu a Mulungu, Mulungu andithandize ine usikuuno, ine ndikhoza kutsimikizira kwa inu kuti iwo onsewo akulakwitsa. Onsewo opembedza *Lamlungu* ndi osunga sabata. Iwo ali mwamtheradi kulakwitsa malingana ndi Mawu. Ndipo pambuyo pa zonse, ndi Mawu omwe ife tiyenera kuti tizipita nawo, osati ndi zomwe a Adventist anena, kapena osati ndi zomwe Achiprotestanti anena, kapena Akatolika anena. Ndi zomwe Baibulo linena.

⁸⁷ Tsopano, tsopano penyani.

Pakuti iye anayankhula mu malo ena ake za tsiku lachisanu ndi chiwiri motere, . . .

Tsopano ife tikuti tiyike chinachake monga *chonchi*, ndi kuchitcha ichi—ichi, “Mpumulo wa Mulungu,” tsiku lachisanu ndi chiwiri.

⁸⁸ Tsopano penyani. “Ndipo Mulungu...” Mvetserani kwa Lemba ili tsopano.

...Mulungu anapuma tsiku lachisanu ndi chiwiri ku ntchito zake zonse.

Mulungu anali ndi Sabata, ndipo tsiku lachisanu ndi chiwiri ilo linali utali wa zaka chikwi chimodzi, choimira cha Zakachikwi.

Pakuti iye anayankhula...za tsiku lachisanu ndi chiwiri motere, Ndipo Mulungu anapuma...ku zake zonse—ntchito zake.

Puronauni yaumwini, “Ntchito Zake zonse.” Iye anapuma pa tsiku lachisanu ndi chiwiri. Uyo ndi Mulungu.

Ndipo mu malo awa, pansu pa lamulo, Ngati iwo ati akalowe mu mpumulo wanga.

⁸⁹ Mulungu anapuma, mwathupi, pakuti Iye anali atapanga miyamba ndi dziko lapansi mu masiku asanu ndi limodzi, ndipo pa tsiku lachisanu ndi chiwiri Iye anapuma ku ntchito Zake zonse. Iye anapuma zaka chikwi chimodzi. Chifukwa Baibulo limanena, kuti, “Tsiku limodzi padziko lapansi liri zaka chikwi Kumwamba; zaka chikwi Kumwamba; ndi tsiku limodzi pa dziko lapasi.” Ndi angati akudziwa kuti Lemba limanena zimenezo mu Petro Wachiwiri? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Chabwino. “Mulungu anapuma pa tsiku lachisanu ndi chiwiri. Ndipo Iye anayankhula motere pa malo ena.”

⁹⁰ Tsopano mvetserani mwacheru.

Pakuti iye anayankhula mu malo ena za tsiku lachisanu ndi chiwiri motere, Ndipo Mulungu anapuma...ku ntchito zake zonse.

Ndipo mu malo awa kachiwiri, lamulo, Ngati iwo ati akalowe mu mpumulo wanga.

Iye anawapatsa Ayuda, pa njira yawo kuchokera ku dziko lamalonjezo...kapena akuchokera ku Igupto, kupita ku dziko lamalonjezo, sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri.

⁹¹ Tsopano mvetserani.

Powona chotero kuti kwatsalira kuti ena alowe mmenemo, ndi kwa iwo omwe unalalikidwa poyamba...

Mpumulo! Mulungu anawapatsa iwo lamulo, ndipo sabata linali lamulo lachinai.

...sanakalowe umo chifukwa cha kusakhulupirira:...

⁹² Tsopano penyani. Iye akuyankhula za lamulo, momwe iwo anakalowera umo, sizinasakanizidwe ndi chikhulupiriro. Iwo sanausunge iwo. Iwo ankasunga sabata mwachikumbutso, kuti iwo anali kupita ku dziko la sabata, kuti akakhale ndi mpumulo wosatha atachoka ku mavuto awo onse ndi zodandaula zawo zonse, kopanda konse owagwiritsa ntchito, kopandanso usiku wosapumika. Iwo anali panjira yawo waku dziko lamalonjezo la mpumulo. Ilo linkayenderera ndi mkaka ndi uchi. Mphesa zinali zazikulu kwambiri mwakuti amuna awiri ankanyamula phava limodzi pa mapewa awo. O, dziko lake la mpumulo wodalalo! Koma iwo analephera kuti alitenge ilo pamene iwo anafika kumeneko, chifukwa cha kusakhulupirira kwawo. Iwo anatembenukira kwina, pa mailosi makumi anai okha kuchokera kumene iwo anachokera ku Igupto, kuti akafike ku dziko lamalonjezo. Ndipo iwo anali zaka makumi anai kuti akafike kumeneko, chifukwa cha kusakhulupirira kwawo. Mulungu anawapatsa iwo mneneri wawo, anamupatsa iye chizindikiro Chake, anamupatsa iye Lawi la Moto, anawonetsa zizindikiro ndi zodabwitsa, ndipo analalikira Uthenga kwa iwo. Ndipo iwo ankapita uko, potsatira nsomba ndi mikate, ndipo anagwera mu chipululu. “Ndipo matupi awo anawonongekera mu chipululu.”

⁹³ Yesu, pa kasupe, Iye ananena.

Anati, “Makolo athu ankadya mana mu chipululu, kwa zaka makumi anai.”

⁹⁴ Iye anati, “INE NDINE Mkate wa Moyo umenewo womwe unabwera kuchokera kwa Mulungu Kumwamba. INE NDINE Mkate wa Moyo. Mose sankakupatsani inu Mkate umenewo. Atate Anga ankapereka Mkate umenewo. Ndipo INE NDINE Mkate umene wabwera kuchokera kwa Mulungu Kumwamba. Ngati munthu adya Uwu, sadzafa konse.” Ndi uko Kusiyana kwake.

⁹⁵ Tsopano penyani. Iwo ananena kuti Iye. . . “Iwo ankamwa kuchokera mu Thanthwe lomwe linali mu chipululu, kwa danga la zaka *zochuluka-kwambiri*.”

⁹⁶ Iye anati, “INE NDINE Thanthwe limenelo.” Lidalitsike Dzina Lake Loyera! “INE NDINE Thanthwe limenelo.”

Iye angakhoze bwanji kukhala Thanthwe limenelo? Thanthwe limenelo linali Thanthwe lauzimu. Ilo linkawatsatira ana a Israeli. Ndipo Mose anali ndi ndodo mu dzanja lake, yomwe inali ndodo ya chiweruzo ya Mulungu. Ndipo Mulungu anamuza iye kuti alikanthwe Thanthwelo, ndipo iye analikantha Thanthwelo. Ndipo pamene iye anatero, madzi anabwera kuchokera mu Thanthwelo. Ndipo Khristu anali Thanthwe limenelo, ndipo chilango cha chiweruzo cha Mulungu cha tchimo chinakanthidwira pa Iye. “Mulungu anapangitsa kuti kuyikidwe pa Iye kusaweruzika kwa ife tonse,” ndipo

kusaweruzika kumeneko kunaphulitsa apo mtima Wake. Ndipo kuchokera mu mtima Mwake anatsanulira Mzimu Woyera, monga mitsinje ya madzi, kwa anthu owonongeka, akufa.

“INE NDINE Thanthwe limenelo lomwe linali mu chipululu.”

“Bwanji,” Iye anati, “Iwe ukutanthauza kuti utiuze. . .”

⁹⁷ Iye anati, “Mose, yemwe anakuuzani inu zimenezoyo, iye ankakhumba kuti aliwone tsiku Langa. Ndipo iye analiwona ilo mwa kagawo.”

⁹⁸ Iye anati, “Tsopano, Iwe ukutanthauza kuti utiuze ife kuti Ndiwe wamkulu kuposa Mose? Kuti Iwe unamuwona Mose? Ndipo Mose wakhala atafa kwa zaka mazana asanu ndi atatu.” Anati, “Tsopano ife tikudziwa kuti Iwe uli ndi mdierekezi,” mwa mawu ena, “wopenga.” “Ife tikudziwa kuti Ndiwe wopenga.”

⁹⁹ Iye anati, “Asanakhalepo Abrahamu, INE NDINE. Ine ndinali INE NDINE WAMKULU yemwe anali mu chisamba choyaka. Ndine Moto umenewo womwe unali mu chisamba choyaka. Ndine Mngelo ameneyo yemwe ankapita patsogolo pawo.” Ndipo Iye anati, “Ine ndinabwera kuchokera kwa Mulungu, ndipo ine ndikubwerera kwa Mulungu.” Ndipo Iye anabwera kuchokera kwa Mulungu, anapangidwa thupi nakhala pakati pathu; anabwerera ku Lawi la Moto lomwe lija.

Ndipo Iye ali pano, usikuuno, zitatha zaka zikwi ziwiri, “yemweyo dzulo lero, ndi kwanthawizonse,” akuchita chinthu chomwecho, kuwatsogolera ana Ake odala.

¹⁰⁰ Ndipo ochuluka akubwera. . .umo chifukwa cha kusakhulupirira. Tsopano, iye anati, “Iye anayika tsiku,” tsiku la pamene Mulungu anatsiriza ntchito Yake. Ndiye, “Iye anayika ‘tsiku lina,’ ndipo motere, kuti ngati iwo ati adzamve, ngati iwo ati adzabwere, omwe asunga sabata, kupitirira nazo kudutsa mu za mwezi watsopano ndi zina zotero.” Apo ndi pamene abale a Advent amayesera kukutengerani inu mmbuyo.

¹⁰¹ Tsopano tiyeni tiwerenge mopitirira. Zindikirani.

Powona chotero. . .kuti ena ayenera kuti alowe umu, ndi iwo kwa omwe poyamba kunalalikidwa sanakalowemo umu chifukwa cha kusakhulupirira.

¹⁰² Tsopano, ndime ya 7. O, mai! Ine ndikuti, Lemba ndi lodzozedwa mwamasamu. Ine ndikuti, Lemba liri, ndipo mwa njira iliyonse, nlodzozedwa. Masamu a Baibulo ndi angwiwo.

¹⁰³ Kodi inu munazindikira United States uyu ali nambala satini mu chirichonse chomwe iye amachita? Inu mukudziwa kuti iye anakhazikitsidwa ndi zigawo satini? Inu mukudziwa mbendela inali ndi nyenyezi satini poyamba? Inu mukudziwa chirichonse chomwe United States amachita chiri mu chiwerengero cha satini? Kodi inu mumadziwa kuti iye amapezeka mu Baibulo mu Chivumbulutso satini? Ndithudi

ali. Kachiroombo kakang'ono, mwanawankhosa yemwe anadza kuchokera pa madzi, osati khwimbi ndi unyinji wa anthu, . . . osati kuchokera mmadzi, koma kuchokera pa mtunda pomwe palibe aliyense. Iye anali ndi nyanga ziwiri zazing'ono: mphamvu yadziko ndi yachipembedzo. Ndipo iye anali mwanawankhosa: ufulu wachipembedzo. Ndipo patapita kanthawi, izo zinapita limodzi ndipo iye ankayankhula ngati chinjoka, ndipo ankachita mphamvu ndi zonse zomwe Roma ankachita asanaye iye. Izo zikubwera ku fuko lathu. Inu muzilembe izo. Inu mupenye mpaka ku Chitaganya cha Mipingo ndi Katolika akulumikizana limodzi. Muwone zomwe ziri nkuchitika.

¹⁰⁴ Anthu omwe akutsatira Lawi la Moto ndithudi adzakhala nayo nthawi yovuta, koma iwo ali okonzekera kusinthidwa pa nthawi imeneyo, ndiko kulondola, okonzekera basi kuti azipita. “Pakuti Mwanawankhosa anawagonjetsa iwo,” linatero Baibulo, “ndi iwo omwe ankamutsatira Iye, chifukwa iwo anali kutchedwa osankhidwa ndi okhulupirika, Osankhidwa a Mulungu.” Tisiye kupita mu uneneri umenewo tsopano, kuti ife tikhoze kupititsa izi pasogolo.

¹⁰⁵ Mvetserani mwatcheru, mutu wa 7, a . . . ine ndikutanthauza mutu wa 4, ndime ya 7. Seveni ndi nambala ya kutsirizitsa. Firii ndi nambala ya Moyo. Seveni ndi nambala ya kutsirizitsa, ndipo iyi ikupereka sabata yamphumphu.

“Ndipo kachiwiri,” kumbukirani, iye anayankhula, “Mulungu,” motere. Ndiye iye anayankhula za “lamulo,” motere. Ndipo kenako, kachiwiri, “Iye anayika tsiku,” tsiku lachitatu, nthawi yachitatu.

Kachiwiri, iye anayika tsiku, tsiku lina, ponena mwa Davide, Lero, itapita nthawi yaitali chotero; . . . Lero, itapita nthawi yaitali chotero; monga izo zinanenedwa, Lero ngati inu mumva mawu ake, musaumitse mtima wanu.

Penyani, ngati Yesu anawapatsa iwo mpumulo (sabata), . . . iye sakanati mtsogolo mwake ayankhule za tsiku lina.

Nyengo zimasintha ndi Yesu Khristu: kuchokera ku lamulo kupita ku chisomo, kuchoka ku ntchito kupita ku chisomo, kuchokera ku chinachake chimene iwe ukuchita kupita ku chinachake chimene Mulungu anachita, pa zokuyenereza zako kapena pa zokuyenereza Zake. Izo zinasintha.

¹⁰⁶ Pamene Mose anabwera kuchokera mu chipululu, ndi lamulo, iye anati, “Inu musati muzichita chigololo. Inu musati muziba. Inu musati muzipha. Muzisunga tsiku la sabata loyera.” Pamene Yesu anabwera kuchokera ku chipululu . . . Pamene Mose anabwera, Mdierkezi anamuyesa iye. Mwamsanga pamene Mdierkezi anamuyesa iye, iye anagonjera kwa izo. Mose

anali ndi malo ofooka. Ndi angati akudziwa chomwe iwo anali? Kupsyamtima. Ndipo mwamsanga pamene iye anawawona iwo akupembedza mwana wang'ombe wagolide, iye anaponyera pansi malamulo ndipo anawaswa iwo, kukusonyezani inu kuti unsembe ukanati udzaswedwe. Ndipo Mulungu anawapereka iwo kwa iye kachiwiri.

¹⁰⁷ Koma pamene Yesu ankabwera kuchokera ku chipululu, masiku makumi anai a kusala, Iye anali wanjala, malo okha ofooka omwe Iye anali nawo. Ndipo Mdierekezi anabwera kwa Iye ndipo anati, “Ngati Iwe uli Mwana wa Mulungu, sandutsa miyala iyi ikhale mkate. Chita chozizwitsa pano. Ndirole ine ndikuwone Iwe ukuchita izo, ndipo ine ndikukhulupirira Iwe.”

¹⁰⁸ Yesu anati, “Zinalembedwa, ‘Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mawu alionse atuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu.’” Iye anadziwa kuti iye sanakomane ndi Mose apo, pakuti Iye anapita ku Mawu.

¹⁰⁹ Anamutengera Iye pa malo okwera, kachisi, anati, “Ngati Iwe uli Mwana wa Mulungu, dziponyere Wekha pansi.” Ndipo *anakutira*, osati kubwereza, koma anakutira Lemba. Anati, “Izo zinalembedwa, ‘Iye awapatsa angelo ulamuliro, zokhudza, kuwopa kuti nthawi iliyonse Iwe, upunthwitse phazi lako kwa mwala. Iye akunyamula Iwe mmwamba.’”

¹¹⁰ Ndipo Yesu anapita molunjika ku Mawu, ndipo anamudzudzula iye.

¹¹¹ Anamutengera Iye pa phiri ndipo anamusonyeza Iye United States ndi Germany ndi Switzerland, ndi mafuko onse a mdziko, omwe akanati adzakhalepo konse, anati, “Iwo onse ndi anga. Ine ndimachita nawo chirichonse chomwe ine ndingafune.” Palibe zodabwitsa kuti ife tikumakhala nazo nkhondo ndi mavuto. Anati, “Ine ndimachita nawo. . .” Palibe zodabwitsa kuti akazi amavala. . . ndi kumapitirira nazo, ndi lamulo. Iwo onse ndi olamuliridwa ndi Mdierekezi. Ndi chimene Baibulo linanena. Satana anati, “Iwo ndi anga. Ine ndimachita nawo iwo chirichonse chimene ine ndikufuna kutero.” Anati, “Ngati Iwe uti undipembedze ine, ine ndikupanga Iwe mfumu monga ine ndiri.”

¹¹² Yesu anati, “Izo zinalembedwa, ‘Iwe uzipembedza Ambuye Mulungu wako yekha, iwe uzimutumikira iye.’ Pita iwe kumbuyo Kwanga, Satana.”

Bwanji? Yesu ankadziwa kuti Iye akanati adzalowe ufumu kwa iwo mu Zakachikwi zazikulu izi, pamene Ufumu Wake ukanati udzabwere. “Kufuna kwanu kuchitidwe pa dziko lapansi monga ziriri Kumwamba.” Uko sikudzakhala kulinso ovala zazifupi. Uko sikudzakhala kulinso kumwa. Uko sikudzakhala kulinso kukhumbira. Uko sikudzakhala kulinso chigololo. Uko sikudzakhala kulinso imfa. Uko sikudzakhala kulinso chisoni. Iye ndi wodzalowa ufumu kwa fuko lirilonse.

Iwo ndi Ake. Ndiko kulondola. Iwo ndi Ake, ndipo Iye adzalowa ufumu. Koma Satana ali nawo iwo kwa danga la nthawi, iyo ndi, tsiku lomwe ife tiri kukhalamoli.

113 “Koma Iye anayika tsiku, kuti, ‘Lero, patapita nthawi yaitali chotere.’ Ndipo anati, ‘Musaumitse mtima wanu.’”

*Pakuti ngati Yesu akanati awapatse iwo mpumulo, . . .
kodi iye sakanatero mtsogolomo kuyankhula za tsiku
lina.*

114 M'bale wanga wa Chiadventisti, yang'ana pa Izo. Paulo apa, anati. Ndipo Paulo anati, mu Agalatia 1:8, ngati inu mukuwalemba apo malembawa, Agalatia 1:8, “Ngati Mngelo wochokera Kumwamba abwera ndi kudzalalikira uthenga wina uliwonse pambali pa Uwu umene ine ndaulalikira, musiyeni iye akhale wotembereredwa.” Paulo anati, “Ngati Yesu akanati awapatse iwo tsiku la Mpumulo . . .”

115 Penyani, pamene Iye anatsika pa phiri. Iye anabwera pansu ndiye. Iye anali atamugonjetsa Mdierekezi. Iye anali atadzozedwa, wokonzekera utumiki Wake. Iye anati, “Inu mumawamva iwo akunena, iwo anthawi zakalewo, ‘Inu musati muzipha,’ koma ine ndikunena kwa inu kuti aliyense yemwe amukwiwira m'bale wake, popanda chifukwa, wapha kale. Inu munawamvapo iwo akuti, iwo a nthawi zakale,” tsiku lino, osunga-sabata. “Inu mwawamvapo iwo akuti, kumbuyo uko a nthawi zakale, pansu pa lamulo. ‘Inu musati muzichita chigololo; ankayenera kukhala mu kuchitako, kuti akhale wochimwa.’ Koma ine ndikunena kwa inu, kuti aliyense yemwe ayang'ana pa mkazi ndi kumusilira iye wachita chigololo ndi iye kale mu mtima mwake.” Zosiyana! Anadutsa apo pomwe ndi lamulo lachinai ilo. Koma kodi Iye anawapatsa iwo Mpumulo?

116 Tiyeni tiwone zomwe iye ananena. “Davide anati, ‘Patapita nthawi yaitali chotere, kudzakhala Mpumulo wangwiro udzabwere.’ ‘Mulungu anapuma ku ntchito Zake, pa tsiku lachisanu ndi chiwiri.’ Mulungu analidalitsa tsiku lasabata, ndipo analipereka ilo kwa Ayuda mu chipululu, motere. Iwo anakalowa umo. . . chifukwa cha kusakhulupirira, chifukwa Mawu sanawasakanize ndi chikhulupiriro. Ndipo kachiwiri, Iye anayika tsiku lina, kunena mwa Davide, ‘Itapita nthawi yaitali chomwecho.’”

Mazana a zaka Davide atafa, Mwana wa Davide akanati awukepo, yemwe ali Yesu, “Ndipo ngati iwo ati amve Mawu Anga, musati muumitse mtima wanu.” Mulungu akuti ayankhule kwa mtima.

117 Tsopano penyani, kwa ndime ya 9 tsopano, kwa inu omwe mukuwerenga. “Yesu akanati adzawapatse iwo mpumulo,” ndime ya 8, “Iye akanati . . . ayankhule za tsiku lina.”

118 Ngati kunali koti kuzikhala sabata, ngati kunali koti kuzikhala kusunga Lamlungu, ndiye Iye akanati ayankhule

za ilo. Ngati Iye akanati, “Tsopano palibenso sabata, palibenso kusunga tsiku lachisanu ndi chiwiri, chimene ine ndikufuna nkuti inu muzisunga Lamlungu,” Iye akanati anene izo. Paulo anati Iye akanatero. Iye akanati, “Inu nonse muzipembedza Lamlungu. Umenewo ukanakhala mpumulo.” Chabwino, ngati iye akanafuna kuti iwo azisunga sabata, iye akanati, “Ingokhalani mukusunga tsiku lachisanu ndi chiwiri. Koma tsopano ine ndikufuna kuti inu muzisunga Lamlungu, tsiku lachisanu ndi chitatu.” Ayi. Iye sananene konse izo.

¹¹⁹ Iye anati, “Ngati Yesu akanawapatsa iwo tsiku, kodi Iye sakanati ayankhule za ilo?”

¹²⁰ Tsopano ndime ya 9. Khalani okonzeka.

Kwatsala chotero mpumulo kwa anthu a Mulungu, kusunga-sabata kwa anthu a Mulungu.

Pakuti iye amene walowa mu wake (wa Khristu) mpumulo, iye nayenso watha ku ntchito zake zomwe, momwe Mulungu anachitira ku zake, pa sabata.

¹²¹ Mukuziwona izo? Tsopano tiyeni titenge Malemba ena ndi kuyikira izi kumbuyo. Chabwino. Pamene Mulungu anapanga dziko mu masiku asanu ndi limodzi, Iye anapuma pa tsiku lachisanu ndi limodzi, ndipo sanagwire konse ntchito kenanso. Lodala likhale Dzina la Ambuye. Iye anamanga dziko, anaika chirengedwe pa ilo, ndipo anapita kukapuma; ndipo sanabwererenso kachiwiri, kuti adzamange dziko linanso. Iye anatsirizitsa ntchitozo, ndipo anapita kukapuma. Tsopano, pa . . . Ndiye, zitatha zaka chikwi izo, ndiye tchimo linabwera umo; ndiye Khristu anaimiridwa, Mwanawankhosa anaimiridwa. Tsopano, Ayuda anapatsidwa ichi ngati choimira cha Mpumulo wa tsiku lachisanu ndi chiwiri.

Tsopano, iye anayika tsiku lina, pakunena mwa Davide, . . . patapita nthawi yaitali chotero, pali kubwera mpumulo wina.

¹²² Tsopano kodi Mpumulo umenewo ndi chiani? Tatembenezirani ndi ine ku Mateyu, mutu wa 11, ndipo gawo lotsiriza la mutu wa 11 wa Mateyu Woyera. Ndi pamene Yesu anatsirizira ulaliki Wake wa pa phiri, ndipo inu muwona zomwe Iye ananena.

¹²³ Iye anati, “Aliyense yemwe ayang’ana pa mkazi, nasilira pa iye, wachita naye kale chigololo mu mtima mwake. Aliyense yemwe amukwiya m’bale wake, popanda chifukwa, wamupha m’bale wakeyo.” Zinthu zonse izi, ndipo Iye sanalikhudze konse lamulo lachinai ilo, sabata ilo.

¹²⁴ Tsopano Iye akutsirizitsa. Ndipo Sabata ndi Lonjezo lalikulu la Mulungu. Ndi Mpumulo. Tsopano, tsopano penyani apa, pamene Iye anatsiriza chiphunzitso cha pa phiri. Apa Iye akuti,

ndime ya 27 ya mutu wa 11 wa Mateyu Woyera. Pamene, Iye anali kuphunzitsa chiphunzitso cha pa phiri mu mutu wa 5.

Zinthu zonse zaperekedwa mu dzanja langa, kwa ine ndi Atate wanga: ndipo palibe munthu amadziwa Mwana, koma Atate; . . .

Mukuona, inu simungakhoze kumudziwa wina popanda kumudziwa winayo, chifukwa Iye anali Atate akuwonetseredwa mu thupi.

. . . ngakhale wina samawadziwa Atate, kupatula Mwana, . . .

¹²⁵ Zikuwoneka ngati anthu akanakhoza kuziwona Izo ndi kusatsutsa. Ndithudi. Mulungu si Anthu atatu. Ngati Iye ali Amulungu atatu, ndiye ndife achikunja. Ndi uti yemwe ali Mulungu? Iwo ali, atatu onsewo, Mulungu mmodzi, ndi maudindo atatu a Mulungu yemweyo. Iye anali Atate, mu mawonekedwe a Mzimu Woyera, mu Lawi la Moto lija mu chipululu. Iye anali Mwana, pamene Iye anagwiritsa ntchito udindo wa Umwana. “Kanthawi pang’ono ndipo dziko silindiwona ine kenanso; ine ndichokapo. Ine ndidzabwereranso ndi kudzakhala ndi inu, ngakhale mkati mwanu, mpaka kumathero a dziko.” Mukuona? Iye ndi Utate, Umwana, Mzimu Woyera, aponso. Izo zonse ndi Mulungu yemwe yemweyo akugwira ntchito mu maudindo atatu osiyana: Utate, Umwana, Mzimu Woyera. Sindizo . . .

Yohane Woyamba 5:7 anati, “Alipo atatu omwe amachitira umboni Kumwamba: Atate, Mwana, Mzimu Woyera. Atatu awa ali Mmodzi.”

¹²⁶ Tomasi anati kwa Iye, “Ambuye, tiwonetsereni ife Atate. Izo zikanamukhutitsa iye.”

¹²⁷ Iye anati, “Ine ndakhala ndi inu motalika chotere, ndipo inu simukundidziwa Ine?” Anati, “Pamene inu mukundiwona Ine, inu mukuwawona Atate. Ndi chifukwa chiyani ukuti, ‘Tiwonetsereni ife Atate?’”

¹²⁸ Tsopano, Aumodzi anazitenga izo, gulu laumodzi la anthu, ndipo amayesera kuwapanga Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, basi udindo umodzi ndi malo amodzi, ndi monga chala chanu, chimodzi. Uko nkulakwitsa. Mulungu sakanati . . . Yesu sakanati akhale atate wa Iyemwini. Ngati Iye akanakhala, ndiye Iye akanati . . . Chabwino, Iye akanakhoza bwanji kukhala atate wa Iyemwini?

¹²⁹ Ndipo ngati Mulungu ali munthu, wapadera kwa Mzimu Woyera, Iye anali ndi atate awiri. Pakuti Baibulo linanena, kuti, “Mzimu Woyera unamufungatira Maria ndipo iye anaima, ndipo,” Baibulo linanena, mu Mateyu 1:18, kuti, “chinthu icho chomwe chikuyembekezeredwa mwa iye ndi cha Mzimu Woyera.” Ndiye atate Ake ndi ati, Mzimu Woyera kapena

Mulungu? Onsewo, ndi Mzimu womwewo, kapena Iye anali ndi kubadwa kwapathengo mwa mizimu iwiri.

Icho ndi chiphunzitso cha Chikatolika, ndipo sichinayambe chakhala chiphunzitso cha Baibulo. Marteni Lutera anabwera nazo kunjira, ndi Chikatolika china chochulukira chomwe chiri mu mpingo wa Chilutera. Wesile anatsatira limodzi nazo. Ndipo izo zikupitirira panobe, koma izo ndi zolakwika. Izo si Choonadi. Sizinayambe zakhala ziri, sizinayambe zakhala ziri Chiphunzitso cha Baibulo. Sizinayambe zakhala ziri lamulo mu Baibulo, kuti aziphunzitsa Amulungu atatu.

Pali Mulungu mmodzi. Yesu anati, “Mverani inu, O Israeli, Ine ndine Ambuye Mulungu wanu, Mulungu mmodzi,” osati Amulungu atatu.

¹³⁰ Mu Afrika, iwo amabatiza kamodzi kwa Atate, kamodzi kwa Mwana, ndi kamodzi kwa Mzimu Woyera. Ndiyeno Myuda wosauka amabwera, nati, “Ndi mmodzi uti wa iwo yemwe ali Mulungu wanu? Ndi uti yemwe ali, Atate, Mwana, kapena Mzimu Woyera?” Iwo, onse atatu, ali Mmodzi. Baibulo limati iwo ali Mmodzi.

¹³¹ Yesu anali nyumba yomwe Mulungu anali kukhalamo. Baibulo limanena zimenezo, kuti, Timoteo Woyamba 3:16, “Popanda kutsutsana,” ndizo, “kukangana, chinsinsi cha umulungu ndi chachikulu. Pakuti Mulungu anawonetseredwa mu thupi, anawonedwa ndi Angelo, analandiridwa po... analalikira, anakhulupiriridwa, ndipo analandiridwa mu Ulemerero.” Mulungu anatero. Baibulo limati, “Dzina Lake adzatchedwa *Emanuele*, lomwe liri mwa kutanthauzira, ‘Mulungu nafe.’” Baibulo linanena, kuti, “Yesu, mwa Iye munkakhala chidzalo cha Umulungu mu thupi.”

¹³² Monga ife tinali nazo izo usiku wina: Mulungu, pachiyambi, anali Mzimu. Ndiyeno, kuchokera kwa Mulungu, kunatuluka Logos, kapena fiofane, chomwe chinali mawonekedwe a munthu, wotchedwa Mwana wa Mulungu, maonekedwe oyambirira. Iye anabwera mu dziko lapansi, mu thupi la mnofu, ngakhale Iye asanabwere mwa Yesu Khristu. Tsopano mezani izo kamodzi, m’bale. Ine nditsimikizira izo kwa inu.

¹³³ Pamene, pamene Mose anamuwona Iye. Iye anati, “Ndiroleni ine ndiwone mawonekedwe Anu, Ambuye.” Ndipo Mulungu anamubisa iye mu thanthwe. Ndipo pamene Iye ankadutsa apo, iye anati, “Iyo inali mbali ya kumbuyo ya munthu.” Iyo inali fiofane. Ndizo ndendende.

Ndiye, fiofane imeneyo inkayenera kuti ipangidwe ya mnofu. Osati Munthu wina, koma Munthu yemweyo ankayenera kuti akhale wa mnofu, kuti adzachotse mbola kwa imfa.

Monga njuchi pamene iyo iluma, iyo imasiya mbola. Ndipo iye sanasiye izo... Iye akanakhoza kuika mbola mu mnofu wa munthu chifukwa iwo ndi tchimo. Koma, m’bale, pamene iye

analuma mnofu wa Emanuelele uja, iye anataya mbola yake. Inde, bwana. Iye akhoza kupanga phokoso koma iye alibe mbola panonso.

¹³⁴ Palibe zodabwitsa, Paulo, pamene iwo ankapita kuti akamudule mutu wake, anati, “O imfa, mbola yako ili kuti? Iwe ukhoza kupanga phokoso ndi kuyimba mochuluka momwe iwe ungafunire. Manda, chigonjetso chako chiri kuti? Koma zikomo akhale kwa Mulungu yemwe akutipatsa ife chigonjetso kudzera mwa Yesu Khristu.” Ndi inu apo.

Izo zinatengera Mulungu Mwiniwake kuti achite izo. Iye anabwera ndipo anawonetseredwa mu thupi. Iye anabwereranso mu Mzimu.

¹³⁵ Inu mukuti, “M’bale Branham, inu simunatiuze ife, panobe, liti pamene Mulungu anapangidwa thupi Iye asanabwere mwa Khristu.”

Pamene Abrahamu anali atakhala pansu pa hema, tsiku lina, uko kunabwera Angelo awiri ndi Mulungu, akudza apo kwa iye, mu mnofu wa munthu. Iwo anali ndi fumbi pa zovala zawo ndipo anali atatopa, ndipo iwo anakhala pansu. Ndipo Abrahamu anapita uko ndipo anakatenga mwana wang’ombe kumuchotsa ku yamanthu, ndipo anamupha iye. Ndipo anapangapo nthuli za mwanawankhosa. Anapita kunjako ndipo anakatenga... anamuza Sara kuti atengepo ufa wa chimanga ndi kuwusefa iwo, ndi kupangapo zitumbuwa. Ndipo anapezapo batala kuchokera kwa ng’ombe, ndipo anatenga mkaka wa batala. Ndipo anazitengera izo panja apo ndipo anazikhazika izo pansu, ndipo Mulungu anazidya izo.

¹³⁶ Aleluya! Ndicho chifukwa, “Chikhulupiroo changa chikuyang’ana mmwamba kwa Inu, Inu Mwanawankhosa wa Kalvare.”

¹³⁷ Inu mukuganiza kuti icho ndi chinthu chachikulu kwa Mulungu? Mulungu, Yemwe anapanga potashi yense ndi kashiamu, ndi chirichonse mu dziko, Iye anabwera pansu kudzamuchezera Abrahamu. Iye anati, “Inu mukuganiza kuti Ine ndikubisilani inu izo, powona kuti ndinu wolandira dziko?” Amen. “Ine sindibisila izo kwa iwe.” Mulungu anangotenga...

¹³⁸ Ife tinapangidwa kuchokera ku zipangizo sikisitini. Iye anangotengapo potashi, ndi kashiamu, mafuta ena, kuwala kwadziko, “Psyfuu!” “Lowa mmenemo, Gabriele,” thupi!

¹³⁹ “Psyfuu!” “Lowa mmenemo, Wormuwudu.” Iye analowa mmenemo.

Angelo awiri, ochokera Kumwamba!

¹⁴⁰ Mulungu anafikira ndipo anatenga zodzaza dzanja za izo, “Psyfuu,” analowa mmenemo, Mwiniwake. Anabwera pansu, ndipo anali ndi njala. Adalitsike! Nanga bwanji zimenezo, abale a Achiadventisti omwe sangadye nyama? Ife tilowa

mu zimenezo, pakapita kanthawi. Mulungu Wamphamvuzonse, Yehova, fufuzani ngati Dzina lomwelo siliri kutanthauza Uyo yemwe pa chisamba choyaka! Aleluya!

Ndiyeno Iye anaima padziko lapansi, Iye anati, “Asanakhale Abrahamu, INE NDINE, Uyo yemwe pa chisamba choyaka.” Ndiko kulondola, Elohim, tiwone ngati sali Yemweyo. Iye anali Yemwe anali pa chisamba choyaka.

¹⁴¹ Iye anali Yemwe apa mu kukhalapo kwa Abrahamu, mu thupi la mnofu, yemwe anadya mwana wang’ombe, ndi kumwa mkaka wochokera kwa ng’ombe, ndi kudya batala pa zitumbuwa. Lodala likhale Dzina Loyera la Mulungu! Anayenda mpaka apo pomwe ndipo anati, “Ine sindichoka . . .”

Ndipo Iye anali atatembenuza nsana Wake. Iye anati, “Abrahamu, Ine ndidzakuchezera iwe, ndipo iwe ubala mwana uja. Iwe uli pa usinkhu wa zaka zana tsopano, ndipo Sara ali makumi asanu ndi anai.” Ndipo Sara, ali mu hema, anati, anaseka. Iye anati, “Nchiani chamupangitsa Sara kuti aseke?” Kumbuyo kwa Iye; hema ili pakati pawo.

¹⁴² Abrahamu anati, “Sara, kodi iwe waseka?”

¹⁴³ “Ayi, ine sindinatero.”

¹⁴⁴ Anati, “Inde, iwe watero.” Ndi mtundu wanji wa kuombeza umenewo? Ndi mtundu wanji wa kuwerenga malingaliro womwe unali?

Iye akuchita chomwecho lero. Iye ndi Yehova-yire, Yehova-rapha, yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Iye samalephera konse.

¹⁴⁵ Tayang’anani pa Iye. Apo Iye waima. Anayenda napita apo ndipo anayankhula kwa Abrahamu; ndipo anachokapo, pamaso pake. Ndipo mbadwa yaikulu Abrahamu anati iye “anayankhula pa maso ndi pa maso ndi Mulungu, Elohim,” Mulungu yemweyo. Mukumvetsa izo? Osati Anthu atatu ayi, m’bale. Maudindo atatu a Munthu yemweyo!

¹⁴⁶ Pachiyambi anali yemweyo, Iye anali Mzimu wawukulu uwo, Kasupe komwe kuli choonadi chonse, chikondi chonse, mtendere wonse. Chirichonse chomwe chinali changwiwo chinali mu Kasupe uyu. Ichu chinayamba kupanga thupi, fiofane, mtundu wa thupi lomwe ife timapitako. Osati thupi laulemerero, koma thupi laungero, longa; lokhala ndi mawumbidwe, mawonekedwe.

¹⁴⁷ Nthawi iliyonse ine ndikawona mtengo, ine ndimaganiza, “Mtengo umenewo ndi choimira. Kuli chenicheni kwinakwake.” Mtengo umenewo unapangidwa kuchokera ku chinachake. Luntha linawupanga iwo. Ndipo zonse zomwe dziko ili limachita ndi kunyezimiritsa kwa Zakumwamba. Baibulo linanena chomwecho. Ndipo ngati pali mtengo pano umene uyenera kuti ufe, ulipo wina mu Ulemerero umene sungawonongeke.

¹⁴⁸ Ngati ine ndiwona mwamuna, ine ndikawona banja laling'ono lokondeka, mwamuna ndi mkazake, akuyenda chotsika mu msewu, okoma mtima limodzi. Kodi izo zimanyezimiritsa chiani? Lidalitsike Dzina la Ambuye! Liripo lina Kumwamba lomwe silidzawonongeka. “Ngati msasa uwu wa pansu pano udzasungunuka, ife tiri nawo wina ukutidikira kale, fiofane.”

¹⁴⁹ Ndiye inu mutenge utatu: Mzimu waukulu, ukukhala mwa Mwana, Yesu; Yesu akukhala mu Mpingo. “Pa tsiku limenelo, inu mudzadziwa kuti Ine ndiri mwa Atate, Atate ali mwa Ine, ndi Ine mwa inu.” Zonse zomwe Mulungu anali, Iye anazitsanulira mwa Yesu; zonse zomwe Yesu anali, Iye anazitsanulira mu Mpingo. Ndi inu pamenepo. “Ine mwa Atate, Atate mwa Ine; Ine mwa inu, ndi inu mwa Ine.” Apo pali . . . Ndi limenelo Thupi.

¹⁵⁰ Ndilo lomwe liri vuto kwa mpingo. Iwo aphunzitsidwa kachiphunzitsa kakale kachikazi koseweretsa, ka dona wokalamba ka mtundu wina, amathamanga ndi kukakhala ndi mgonero woyamba ndi nsuzi ndi maphwando a njuga. Palibe zodabwitsa ife tiri nalo gulu la zisokonezo lomwe ife tiri naloli. Ife sitikusowa madongosolo a ana ndi mgonero waung'ono wa nsuzi. Chomwe ife tikusowa ndi Uthenga wakale wolimba, ndi amuna a chikhulupiriro ali ndi lupanga litapachikika pamenepo, ndi kumatsutsa zinazo. Chomwe ife tikusowa lero, osati fioloje ina yowetedwa ndi lingaliro lina la manenedwe lopangidwa ndi munthu wina. Ife tikusowa Uthenga wolama wolalikidwa mwa Kuwala ndi Mphamvu ndi chiwonetsero cha Mzimu Woyera.

¹⁵¹ Zindikirani apa tsopano.

Monga iye ananena, *iyе anayika tsiku lina, pakunena mwa Davide, . . .*

. . . ngati Yesu akanati awapatse iwo mpumulo, . . . kodi iye sakanati. . . ayankhule za tsiku lina.

Koma *pali kutsalira . . . mpumulo kwa anthu a Mulungu.*

Pakuti iye yemwe walowa mu mpumulo wake, . . . watsiriza ku ntchito yake yomwe, monga Mulungu anachitira kwa yake.

¹⁵² Tsopano kodi ife tiwerenga pati? Mateyu, twente- . . . Mutu wa 11, ndime ya 27.

Zinthu zonse zomwe Atate anazipereka kwa ine, zinaperekedwa kwa ine ndi Atate wanga; kani: ndipo palibe munthu adziwa Mwana, koma Atate; chabwino, ngakhalenso palibe wina amadziwa Atate, kupatula Mwana, ndi kwa iye amene Mwana afuna kumuululira iye.

¹⁵³ Taonani, si kuchuluka kwa momwe inu muphunzilira, kuchuluka kwake—abishopu akufunira kuti inu mudziwe. Ndi

kuchuluka kwa momwe Mulungu akufunira kuti inu mudziwe. Ngati inu simungathe kuliwona Vumbulutso ili, musati muwafunse abishopu. Mufunsemi Mulungu. Musati muwafunse abusa anu. Mufunsemi Mulungu. “Mwana amamuwulula Iye,” *Iye*, puronauni yaumwini.

¹⁵⁴ Mvetserani. Izi zikuzizimutsani inu. Apa pali lamulo. Paulo anati, “Ngati Iye akanasiya tsiku lina, Iye akanayankhula za ilo.” Koma apa pali zomwe Iye ananena.

Idzani kwa ine, nonse inu omwe muli kuvutikira ndipo muli olemedwa kwambiri, ndipo ine ndikupatsani inu sabata, mpumulo.

Tengani gori langa pa inu, ndi kuphunzira kuchokera kwa ine; pakuti ndine wofatsa ndi wodzichepetsa mu mtima: ndipo inu mudzapeza sabata kwa moyo wanu.

Pakuti gori langa liri lofewa, ndi katundu wanga ali woepuka.

¹⁵⁵ Penyani zomwe Paulo ananena.

. . . ngati Yesu akanati awapatse iwo mpumulo, . . . iye akanati anene za tsiku lina.

Koma iye anayika . . . tsiku, nati mwa Davide, . . . patapita nthawi yaitali chotere; . . . pamene inu mumva mawu ake, musawumitse mtima wanu.

“Ndipo pali kutsalira . . .” Mvetserani tsopano, ndime ya 9.

Pali kutsalira chotero mpumulo, sabata, kwa anthu a Mulungu.

Pakuti iye, mwamuna kapena mkazi, yemwe walowa mu mpumulo wake . . .

“Bwerani kwa Ine, inu nonse amene mukuvutikira ndi olemedwa kwambiri. Ine ndikupatsani inu mpumulo.”

. . . wapuma kwa zake . . . zintchito, monga Mulungu anatero ku zake.

¹⁵⁶ Inu mukhoza kukhala usinkhu wa zaka makumi awiri. Inu mukhoza kukhala usinkhu wa zaka makumi atatu. Inu mukhoza kukhala usinkhu wa zaka makumi asanu. Koma miniti yomwe inu mumva Liwu la Mulungu likugogoda pa mtima wanu, musati muwuumitse iwo. Ndiye lowani. . . “Iye amene amva Mawu Anga, nakhulupirira pa Iye yemwe anandituma Ine, ali nawo wosatha, Moyo Wamuyaya, ndipo sadzabwera konse ku chiweruzo koma wadutsa kuchokera ku imfa wapita ku Moyo.”

¹⁵⁷ “Mukuti, M’bale Branham, chimachitika ndi chiani?” Iwe umalandira Mzimu Woyera. Khristu amabwera mwa iwe. Ndi kulondola uko?

¹⁵⁸ Tembenuzani ndi ine ku Yesaya, mutu wa 28, ndipo tiyeni tiweringe. Yesaya, mutu wa 28, tiwone zomwe mneneri ananena pa izo. Mateyu. . . 28, kuyambira pa ndime ya 8. Apa pali

kuneneratu kwa masiku otsiriza. Ife tiyenera kuti titseke mu miniti.

Pakuti magome onse adzakhala ali, adzaza ndi masanzi ndipo... palibe malo aukhondo.

¹⁵⁹ Ndiroleni ine ndiime miniti, monga Ernie ananena usiku wina. Iye anali kuyankhula kwa winawake. Ernie Fandler, m'bale uyu apa wochokera ku Switzerland, iye anati, "Ine ndinaina ndi kuzilola izo kuti zilowerere mkati."

¹⁶⁰ Ine ndikufuna izi kuti zilowerere mkati.

... palibe malo aukhondo.

Pakuti magome onse adzakhala ali odzaza ndi masanzi...

Ndipo monga *garu* amabwerera ku *masanzi* ake... *ndi nkhumba... ku matope ake*, chomwechonso anthu amatembenukira mmbuyo.

¹⁶¹ Chavuta nchiani kwa inu Achimethodisti? Inu munayamba mwakakhalapo ndi Kuwala. Chinachitika ndi chiani? Mulungu anakuchotsa Iko mu dzanja lanu ndipo Iye anakupereka Iko kwa Anazarene.

Chinachitika ndi chiani kwa inu Anazarene? Nthawiina inu munali nako Kuwala. Mulungu anakutenga Iko mu manja mwanu ndipo anakupereka Iko kwa Achipentekoste. Kulondola. Inu mpingo wa Mulungu ndi nonse inu anthu achiyero, chifukwa inu munakukana Kuwala, inu munadzipanga nokha chipembedzo ndi kuti, "Ife sitikhulupiriranso zina kuposa *izi*," Mulungu anasunthira kunjwa ndipo anakusonyezani inu kuti Iye anali nawo anthu omwe akanamutsatira Iye.

¹⁶² Chinachitika nchiani ndi inu Achipentekoste? Inu munali nako Kuwala. Mulungu wakuchotsa Iko kwa inu.

Lawi la Moto likusunthirabe mtsogolo. Nthawi iliyonse yomwe Lawi la Moto linkasuntha, Mpingo unkasuntha limodzi Nalo ilo.

Ndipo pamene Lutera anapanga bungwe, kunjwa kwa mpingo wa Chikatolika, mpingo wake womwe, Lawi la Moto linasuntha ndipo Wesile anapita nalo Ilo.

Wesile anapanga bungwe napanga chipembedzo chake, ndipo Lawi la Moto linasuntha ndipo Anazarene anapita Nalo ilo.

Anazarene anapanga bungwe, ndipo mpingo wa Mulungu unapita Nalo ilo; ndipo anati iwo sanali chipembedzo, koma iwo anali.

¹⁶³ Ndiye chinachitika ndi chiani? Chinthu chotsatira chinachitika, Achipentekoste anawuona Motowo, ndipo anapita kutali. Ndipo kodi inu munachita chiani? Munapanga chiphunzitso pa malirime, ndipo munadzipanga bungwe izo,

“Aliyense ankayenera kuti ayankhule mu malirime iwo asanalandire Mzimu Woyera,” ndiye Mulungu anasuntha pomwepo ndipo anakusiyani inu mutakhala pomwe inu mulipo.

¹⁶⁴ Chinachitika ndi chiani kwa inu Aumodzi? Inu munapeza ubatizo, Dzina la Yesu. Inu munapanga chiphunziro pa iwo, ndipo munadzipatula nokha kwa zonse Izo, ndipo Mulungu anachoka apo pomwe nakusiyani inu mutakhala pamenepo. Kulondola.

¹⁶⁵ Chinachitika ndi chiani ndi inu a Assembly of God, General Council yakale? Inu munapanga chipembedzo pa zanuzo, ndipo Mulungu anachoka apo pomwe nakusiyani inu mutakhala. Ndipo tsopano sindinu kanthu koma gulu lozizira, lofunda monga ena onse a iwo ali.

Ndipo Lawi la Moto likusunthirabe patsogolo. Aleluya!

... magome onse adzaza ndi masanzi. . .

¹⁶⁶ Tayang’anani pa Mgonero wa Ambuye. Mwakuti, ngakhalenso iwo ali nawo malo komwe iwo amakatengako mtanda wakale wa buledi. Ndipo mkatewo umayenera kuti uzipangidwa ndi mkate wopanda chotupitsa. Ndipo iwo amawupereka iwo kwa ochimwa, osuta ndudu, aziwerewere, timahule, bola ngati iwo ali nalo dzina lawo pa bukhu.

¹⁶⁷ Ndipo inu Abaptisti mpaka mumautcha iwo mgonero “wodzitsekera.” Tsopano, inu Abaptisti mumadzibwekerera pang’ono, Mulungu adzaichotsapo nyanga yanuyo. Ndiko kulondola ndendende, inu simudzakhoza kuiwomba iyo. Mgonero “Wodzitsekera,” inu mumadzipatula nokha, kuwoneka ngati oyera kuposa ndi momwe muliri.

Kumbukirani, uyu ndi kachisi wa Chibaptisti. Ndi chimene inu mukupeza, inu mukuzipanga nokha bungwe. “O,” inu mukuti, “ife sitiri bungwe.” Inde, inu muli. Ndithudi, inu muli. Inu mukuti, “Ndife chiyanjano.” Eya, aliyense akabwera pakhomo ndi kudzaphunzitsa basi momwe inu mumakhulupiriramo, izo nzabwino. Koma, wina, i—inu simungamuponyere iye panja, koma inu mungamuchotse iye pa ubale wanu. Ndiko kulondola ndendende. O, inu muli nayo njira yochitira izo. Chomwechonso Mulungu ali nayo njira yochitira izo. Koma Mpingo wa Mulungu uzisunthirabe mtsogolo. Lawi la Moto silingaimire zimenezo.

... magome onse ali odzaza ndi masanzi. . .

¹⁶⁸ Tsopano mveterani. Tsopano izi zikunjenjemeretsani inu miniti yokha. Mveterani. Ine ndiwerenga Mawu. Anali ndani uyu? Mneneri, Yesaya.

... magome onse ali odzaza ndi masanzi. . . chotero palibe kanthu kaukhondo, zangokhala garu-kudya-garu.

169 Kubwera ku mpingo: akazi kubudula, kudulapo tsitsi lawo, kuvala zazifupi, kutuluka panja ndi kumawawona amuna akubwera mu msewu; kumatchetcha udzu pabwalo, asungwana aang'ono amafuna kumva winawake akupanga likhweru la garu wamphongo lija kapena la nkhandwe, chirichonse chomwe icho chiri, inu mukudziwa, “Fyu-fyuu!” O, inu mukuganiza kuti ndinu okongola, sichoncho inu?

170 Inu amuna mumayenda mu msewu, muli ndi ndudu pakamwa panu, ndipotu dikoni wa pa gulu. Inu mumawoneka ngati ng'ombe yopanda nyanga yaku Texas. Ndiyeno inu mumaganiza kuti ndinu winawake. Ndiko kulondola ndendende. Palibe zodabwitsa magome onse...Nkuwuka apo ndi kukatenga mgonero, ndi kumachita ngati kuti ndinu winawake, ndi kumanama ndi kuba ndi kunama, mu sabata yonseyo. Chavuta ndi chiani ndi inu?

...magome onse adzaza ndi masanzi...

171 “O, ine ndimatenga Mgonero wa Ambuye. Zedi, ife timachita izo mu mpingo wathu. Yesu anati Iye adzatidzutsa ife mu masiku otsiriza ngati ife tizitenga Mgonero wa Ambuye.”

172 Koma, “Iye amene adya ndi kumwa mosayenera, adya ndi kumwera chiweruzo kwa iyemwini, pa kusalizindikira Thupi la Ambuye. Pa chifukwa ichi ambiri amadwala ndi kufooka pakati panu, ndipo ambiri afa,” mipingo yokalamba, yakufa, ya chizolowezi. Mzimu wa Mulungu wakuchokerani pa inu. Lawi la Moto palibe apo panonso. Inu mukukana machiritso Auzimu. Inu mukukana chiukitsiro.

173 “O,” inu mukuti, “o, Iye anauka kwa akufa, mwambiriyakale.” Chabwino, nanga bwanji za Iye kukhala yemweyo lero, ngati Iye anauka kwa akufa? Inu mukuti, “O, izo siziri chomwecho.” Tsopano, ndi inu apo. Inu muli nacho chiukitsiro momwe inu mukuchifunira icho, ndipo Mulungu ali nacho icho momwe Iye akuchifunira icho.

174 Koma, chinthu chake ndi ichi, Baibulo linati, zomwe ife tikuzidziwa ziri Choonadi, kuti Iye akanati atsimikizire Mawu. “Ndipo zinthu izi zomwe Ine ndikuzichita inu muzidzazichita mofanana. Ndipo Ine ndidzakhala ndi inu nthawizonse, mpaka kumathero a dziko.” “Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Basi chimene Mawu ananena.

175 Tsopano kodi sabata ndi chiani?

...magome onse adzaza ndi masanzi...palibe limodzi laukhondo.

Ndani yemwe iye ati amuphunzitse chidziwitso?

Osati chidziwitso cha chidziko; chidziwitso chauzimu!

Ndani yemwe iye ati amuphunzitse chidziwitso?...
ndani yemwe Iye ati amupangitse...kumvetsa
chiphunzitso?

176 “O, dalitsani Mulungu, bungwe lathu silimakhulupirira Izi. Iwo sakanati apilire nazo Izo.” . . . kusamala zomwe bungwe lanu limakhulupirira. Kodi Mawu a Mulungu amati chiani pa izo? “O, chabwino, azibusa athu, inu mukudziwa, ndi ophunzira.” O, zedi. Ndithudi, ali nawo maphunziro ochuluka kwambiri, iwo anamusiya Mulungu mu zimenezo. Moona, pakuti inu mukhoza kuwauza iwo Mawu ndipo iwo akhoza kungoyenda mozungulira nkuti, “Chabwino, ine sindimawakhulupirira Iwo basi mwanjira imeneyo.” O, inu chinthu chachikazi! Ndiroleni ine ndikuuzeni inu.

177 Yang’anani apa.

. . . ndani *yemwe iye ati amupangitse . . .*
kumudziwitsa chiphunzitsa? Iwo amene aletsedwa ku
bere, ndi . . . iwo amene aletsedwa ku mkaka, ndipo
achotsedwa ku mabere.

178 Tsiku lina, woyandikana nane wanga. Iye anati, “Billy, m’busa winawake muno mu mzinda, munthu wamng’ono wokondeka yemwe inu munayamba mwamuwonapo . . .” Anati, “Akazanga ndi ine tinali titakhala titavala zovala zogonera, pafupi pakati pa usiku, ndipo m’busa wamng’ono uyo anathamangira umo ndipo i—i—iye anamwa nafe khofi ndipo anapita ku nyumba ya oyandikana nawo ena, ndipo anakagwirana nawo chanza. Iwo anali ndi masewero aang’ono a njuga, ndipo iwo anakhala pansu ndi kusewera njuga ndi iwo.” Anati, “O, iye ndi munthu wamng’ono woyanjanika kwambiri yemwe inu munayamba mwamunawonapo.” Anati, “O, ife timamukonda iye. Ife sitikanati timuchotse iye popanda chifukwa.”

179 Ine ndinaima apo pang’ono pokha, ine ndinaganiza, “Chabwino?”

180 Anati, “O, kodi inu simukuganiza kuti mpingo uliwonse ukusowa mwamuna wonga ameneyo?” Nha! Ine sindikanakhoza kuyankha zimenezo. Iye anati, “Mu malo ena aang’ono,” anati, “iwo anali ndi malo okondeka oterowo. Mtumikiyo ndi mkazake, anthu okondeka, amapita kunja ndi kumakachita nawo ana mochuluka kwambiri mpaka iwo anali ndi—sukulu ya Baibulo.” Ndipo anati, “Iwo amangokhala nawo ochuluka kwambiri, anasefukira pamalopo ndi ana aang’ono.” Anati, “Mai, iye amakhoza kunena mitundu yonse ya nthano zazing’ono kwa ana aang’onowo.”

181 Ine ndinati, “Izo nzabwino. Izo ndi zabwino kwambiri.”

182 Ine ndinabwerera kwathu. Ine ndinali nditangofika kumene kuchokera ku Canada. Ine ndinaganiza, “Ndine pano. Mai! Anthu . . . Vuto nechiani ndi ine? Ine sindimachita zimenezo.” Ine ndinapita kumakatsuka galimoto yanga. Ine ndinaganiza, “Mulungu, ine ndikuyamba kukhala bambo wachikulire, ndipo ndine pano. Ine ndamenyera. Ine ndalirira. Ine ndapempha.

Ndipo chirichonse chomwe ine ndimapenza ndi kuchitiridwa mwano kwakukulu.”

183 Chirichonse, winawake amayankhula zoipa za iwe, “O, woyera-wodzigudubuza wokalambayo,” chinachake monga icho.

184 Ine ndinaganiza za izo. Ndipo Liwu linadza kwa ine, linati, “Amuna awo ziri bwino ngati iwo akuchita izo, koma Ine sindinakuitane iwe kuti uzichita zimenezo. Ine ndinakuitana iwe kuti uzitenga Lupanga ndi kumaima apo monga Yoswa ndi kutsutsa nalo, m’bale. Osati kumapulisana apo ndi kagulu kena kakale kapena bungwe lina la mpingo, koma kutsutsana naye Mdierekezi. Kuima patsogolo pomwe, kupangitsa choona kukhala choona, ndi cholakwika cholakwika. Kulalikira Mawu ndi kumupeza yemwe ali nacho chikhulupiriro kuti angawakhulupirire Iwo. Kumuika iye pamene.”

185 Ine ndinayamba kufulumizitsa pa galimotoyo, nthawi yonseyo, ndikuitsuka. Ine ndinati, “Zikomo inu, Ambuye. Zikomo inu, Ambuye.” Ndinamverera bwino ndiye, “Zonse ziri bwino, Ambuye, Ine ndigwiritsa ilo molimbira pang’ono, ndipo ine ndikufuna kuti ndife ndiri Nalo mu dzanja langa.”

...nndani yemwe Ine ndingati ndimudziwitse
chiphunzitsa? (Mvetserani.)

...magome ali odzaza ndi masanzi. . .

...iwo omwe achotsedwa ku mkaka, ndi kuchotsedwa
ku mabere.

Tsopano penyani.

*Pakuti langizo monga ilo pa—pa langizo, langizo
pa langizo; . . . mzere pa mzere; apa pang’ono, ndi apo
pang’ono:*

*Pakuti ndi milomo yachibwibwi ndi malirime ena Ine
ndidzayankhula kwa anthu awa.*

*Kwa omwe izo zinanenedwa, Ili ndilo sabata momwe
inu mudzapangitsa olema kuti apumule; . . . uku ndi
kutsitsimutsa: komabe iwo sakanakhoza kumvera.*

*Pakuti mawu a YEHOVA anadza kwa iwo, winawake
anawalalikira Iwo, langizo pa langizo, . . . pa langizo;
mzere pa mzere, . . . pa mzere; apa pang’ono, ndi apo
pang’ono; kuti akhoze kupita, ndi kukagwera mmbuyo,
ndi kutyoledwa ndi kukodwa ndi kutengedwa.*

186 Kodi Mpumulo ndi chiani? Ndi liti pamene Mpumulo unabwera? Pamene anthu anayankhula ndi malirime ena ndipo anali ndi milomo yachibwibwi. Milomo yachibwibwi; iwo sanali kuyankhula kanthu. Iwo ankachita chibwibwi. Ndi liti pomwe izo zinachitika? Pa Tsiku la Pentekoste, pamene Mzimu Woyera unabwera. Umenewo ndiye Mpumulo: Mzimu

Woyera. Yesu anati, “Bwerani kwa Ine, nonse inu ovutikira ndi olemedwa kwambiri, ndipo Ine ndikupatsani inu Mpumulo. Ine ndikupatsani inu Moyo, Moyo Wamuyaya,” Zoe, Moyo wa Mulungu womwe. Mulungu abwera mwa inu ndipo akhala gawo la inu. Iye akupatsani inu kubadwa ndipo akupangani inu mwana wake wamwamuna ndi wamkazi.

¹⁸⁷ Tsopano penyani. Uwo unali mpumulo wachitatu umene Iye anapereka. Woyamba: Mulungu anawulandira iwo, kuchokera ku ntchito Yake. Wachiwiri: Israeli anawulandira iwo, mu lamulo. Wachitatu: Mpingo unawulandira Iwo, monga gawo la Mulungu.

¹⁸⁸ Firii ndi nambala ya moyo. Ndi angati akudziwa zimenezo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Nthawi iliyonse yomwe inu muwona zitatu, ndi moyo. Zindikirani, pamene Mulungu analenga dziko lapansi, pa tsiku lachitatu kunali moyo. Ndi angati akudziwa zimenezo? [“Ameni.”] Tsiku lachitatu. Uko kunadza moyo pa tsiku lachitatu la kulenga.

Utatu: Atate anali pamwamba pa anthu, mu Lawi la Moto; Mwana anali Munthu, yemwe ankayankhula kwa anthu ndi kuwakonzeketsera iwo; Mzimu Woyera inali sitepe yachitatu, umene unali Mzimu Woyera, Mulungu mkati mwa anthu. Moyo! Atate, Mwana . . .

Mpumulo, wa Mulungu; mpumulo, wa Israeli; ndi Mpumulo, wa Mpingo, kusunga-sabata.

¹⁸⁹ Chotero, ngati inu simunayambe mwalandirapo Mzimu Woyera, panobe, inu simunalowepo konse mu Mpumulo wa Mulungu. Inu simukusowa kuti muzichita kunena, “O, ine sindingakhoze. Ine ndimafuna kuti ndisute. I—ine sindingakhoze basi kuchita izo; ndine Mkhristu. Ine kwenikweni sindikufunadi kuti ndizimwa, koma ndine Mkhristu. Ine sindingakhoze basi, sindikufuna kuti ndizimwa, komabe ine ndikanakonda ndikanatero.”

¹⁹⁰ Ngati inu mumasilira akazi, ngati inu mumachita zinthu zonse zopanda umulungu izi, inu simunagunde nthawi ya Mpumulo iyo panobe. Inu simunalowe nkomwe mu Mpumulo wanu.

¹⁹¹ Ndipo pamene inu mulowa mu Mpumulo uwu, inu mumapuma ku ntchito zanu za chidziko, monga Mulungu anachitira ku Zake. Bwanji? Ndinu gawo la Mulungu. Inu mumapumula, Mwamuyaya. Ndi inu apo. Ilo ndilo Sabata. “Bwerani kwa Ine, nonse inu ovutikira.”

Lero, *iye* anayika *tsiku linalake*, . . . *patapita nthawi yaitali chomwechi*, mwa Davide; . . . *pamene inu mumva liwu lake, musaumitse mitima yanu.*

¹⁹² Mawu kapena awiri okha owonjezera apa tsopano, ife titseka.

Pakuti iye yemwe walowa mu mpumulo wa Khristu, . . .

Bwerani kwa ine, nonse inu ovutikira ndi . . . olemedwa kwambiri . . .

. . . inu mwatsiriza ku ntchito zanu zomwe, monga Mulungu anachitira ku zake, pa tsiku lachisanu ndi chiwiri.

Lanu mwinamwake linali pa chaka chamakumi atatu, chaka chamakumi anai, chaka chamakumi asanu, chirichonse chomwe chiri. Inu mwatsiriza ku ntchito zanu, monga Mulungu anachita ku Zake, Mwamuyaya. Inu simukufunanso zinthu za mdziko. Dziko liri lakufa kwa inu.

¹⁹³ Tsopano, ndime ya 11 tsopano, mwatcheru.

Tiyeni ife tivutikire chotero kuti tilowe mu mpumulo umenewo, (osati uwu, osati uwu, koma Uwu), mwina munthu wina angagwe potsatira chitsanzo cha kusakhulupirira chomwecho.

¹⁹⁴ Ndi chiani chimenecho? Lawi la Moto liri pano. Mngelo wa Ambuye ali ndi ife. Iye akuchita zinthu zomwezo zimene Iye anati Iye akanamadzazichita. Ndipo anthu akumaphunthwa apo, nkumati, “O, chabwino, ine ndikulingalira Izo zonse ziri bwino. Izo nzabwino kwambiri. O, ine ndikulingalira Izo nzabwino.” Khalani osamalitsa kuti inu musagwere mu msampha womwewo wa kusakhulupirira. Inu muzitenge Izo ndi mtima wanu wonse.

¹⁹⁵ Penyani.

Pakuti mawu a Mulungu (osati chiphunzitso cha mpingo) . . . mawu a Mulungu ndi achangu, amphamvu kwambiri, . . . akuthwa, . . . kuposa lupanga lakuthwa konsekonse, (mvetserani), opyoza ngakhale . . . mogawanizira mwa solo, mzimu, . . . molumikizira ndi mmafuta a mmafupa, ndi . . . (mvetserani), ndipo ali ozindikira maganizo ndi zamkati mwa mtima.

Chinali chiani chimenecho? Mzimu Woyera ukhoza kubwera nkuti, “Iwe unachita chinthu *chakuti-chakuti*. Ndipo iwe unachita *ichi* ndipo unachita *icho*. Iwe uli ndi matenda a mtundu *uwu*, ndi *uwo*. Ngati iwe uti uchikonze *ichi*, iwe uchita *icho*.” Mukuona? Ozindikira maganizo.

¹⁹⁶ Ndipo anthu amati, “Ndi chiani chimenecho? Mwakuti, ndi kuwerenga maganizo. Mwakuti, ndizo . . . Iye ndi wambwebwe.” Mukuona zomwe ine ndikutanthauza? Ilo ndi dziko lakale loipa, lachigololo lomwe silikumudziwa Mulungu.

¹⁹⁷ “Iwo ndi achangu, oganizira, amphamvu kwambiri kuposa lupanga lakuthwa konsekonse, ndi ozindikira za mmalingaliro ndi zolinga za mtima.”

Tsopano, nchiani icho chomwe chimadziwa zolinga za mtima? Mulungu. Inu mukuti, “Chabwino, Baibulo linati, ‘Mawu a Mulungu.’” Mawu a Mulungu ndiwo Mulungu.

Pachiyambi panali Mawu, . . . Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu.

Ndipo Mawu anapangidwa thupi, ndipo anakhala pakati pathu, . . .

¹⁹⁸ Mulungu amazindikira maganizo. Abrahamu anali atatembenuza nsana wake, n—ndipo nayenso Mulungu anali atatembenezira nsana Wake ku hema. Ndipo Sara anaseka. Ndipo Mulungu anapotoloka apo, nati, “Nchiani chamupangitsa Sara kuti aseke?” Wozindikira maganizo a mu mtima! Ine ndikufuna kuti izo zilowerere pang’ono pokha.

¹⁹⁹ Ndiye pamene mtundu wa utumiki umenewo uwuka, womwe Mulungu analonjeza mu tsiku lotsiriza, chachitika ndi chiani? “Kuwerenga maganizo.”

²⁰⁰ Kodi iwo sanawatche Ambuye, Mwiniwake, “Belezebabu”? Iye anati, “Ngati akumutcha Mbuye wa nyumba ‘Belezebabu,’ ndi mochuluka bwanji ati adzawatche ophunzira Ake?”

²⁰¹ Ine ndimakukondani inu. Izo zikupita zikusonyeza kuti inu mukusangalatsidwa mokwanira, inu simukusowa kubwera ku nyumba yampweya wabwino kuti mudzamve Uthenga. Ndinu anjala mokwanira kuti mwakhoza kubwera ku malo onga awa. Mulungu sakanatilola ife kuti timange china konse koma ichi. Ife timachikonda icho momwe icho chiriri. Basi kachisakasa kakale, koma umo ndi momwe ife timachikondera icho. Mulungu samakhala mu zonyezimira. Mulungu amakhala monyozeka. Ife timachikonda icho monga chonchi. Ife tikukondwa kumabwerako, ndipo inu muli, nanunso, kudzakhala mu—malo onga awa. Ziribe kanthu momwe muliri motentha, momwe inu mukuchitira thukuta pa suti yanu yatsopano, diresi lanu latsopano, izo sizikupanga kusiyana kulikonse.

Inu mukumvetsera ku Moyo Wamuyaya, kwa Mawu a Mulungu omwe akudziwa maganizo a mtima wanu. Lawi la Moto lomwe linkapachikika pa ana a Israeli, lapachikika pano usikuuno. Ine ndikhoza kutsutsa ena pa izo: palibe munthu angakhoze kuima pano pansu pa mphamvu ya Mzimu Woyera popanda Mulungu kumutsanula iye zonse kuzitulutsa ndi kumuuzza iye chomwe iye anali. Ndiko kulondola. Ndi inu apo.

²⁰² Nchiani Icho? Nchiani Icho? Ndi Mzimu womwewo umene unkawatsogolera Ana a Israeli kupita ku mpumulo wawo, ndipo iwo anagwa chifukwa cha kusakhulupirira. Inu musati mugwe. Uwu ndi mwayi wotsiriza. Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, Moyo umabwera kudzera pamenepo.

²⁰³ Kulungamitsidwa, Marteni Lutera, mawonekedwe a chipembedzo apobe. Kuyeretsewa. . . Marteni Lutera; John

Wesile; ubatizo wa Mzimu Woyera, Moyo. Kulungamitsidwa, ndiko kukhulupirira; kuyeretsedwa, ndiko kuyeretsa; Mzimu Woyera, ndiko kudzazitsa, Moyo. Osati kudzera mu m'badwo wa Chilutera; iwo anali nawo Iwo mwa mawonekedwe. Osati kudzera mu m'badwo wa Wesile; iwo anali nawo Iwo mwa mawonekedwe. Koma uwu ndi m'badwo pamene Mzimu Woyera ukubwera, Iwoweni.

²⁰⁴ Ndipo ngati inu simunaulandire Iwo, mungachite bwanji inu, inu kuti mukhoze kukhulupirira zozizwitsa? Izo zimatengera Mulungu, mkati mwanu, kuti mukhulupirire. Iwe umachita ngati Mulungu. Iwe umadziwa ngati Mulungu. Iwe umaganiza ngati Mulungu. Baibulo linanena kuti inu ndinu ophunzira “timilungu” tating’ono. Yesu ananena chomwecho. Pakuti, ndinu gawo la Mulungu.

Chimodzimodzi monga ine ndiri Branham wamng’ono, ndipo ndinu wamng’ono aliyense yemwe inu muli, ndi chifukwa makolo anu ali dzina limenelo. Chikhalidwe chomwe inu muli ndi chifukwa chakuti makolo anu ali mwanjira imeneyo, chifukwa inu munabadwa mwa iwo.

Ndipo chifukwa chomwe inu mukhulupirira Mulungu, ndi kukhulupirira mu zozizwitsa, ndi zizindikiro ndi zodabwitsa, ndi chifukwa ndinu ana aamuna ndi aakazi a Mulungu. Inu mwalandira Moyo. Moyo umabwera pachitatu. Chabwino.

²⁰⁵ Pamene Yesu anakwera pamwamba pa phiri, kulikonse komwe Iye ankapita, Iye ankamutenga Petro, Yakobo, ndi Yohane, mboni zitatu. Firii ndi nambala ya Moyo. Mukumvetsa izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Chikondi, chimwemwe, mtendere.

²⁰⁶ Tsopano, tiyeni tipite mwamsanga tsopano ku mapeto a mutuwo, mofulumira, pamene ife tikuwerenga.

Pakuti mawu a Mulungu ali achangu, amphamvu kwambiri . . . kuposa lupanga lakuthwa konsekonse, . . . ndi ozindikira ngakhale zolinga za mtima.

Ngakhalenso kuti palibe cholengedwa chirichonse chomwe chiri chosawonekera pamaso pake: koma zinthu zonse ziri . . . zotseguka kwa maso a iye amene ife tiyenera kuchita naye.

²⁰⁷ M’bale, palibe ntchentche yomwe ingatere pa mtengo apo, popanda Iye kudziwa izo. “Zinthu zonse ziri poyera.” M’bale, Iye amadziwa chirichonse chomwe inu munayamba mwachitapo, lingaliro lililonse inu munaliganizapo. Ndi chomwe Iye ali. Ife timamukhulupirira Iye monga choncho.

Ndipo pamene Mulungu abwera mwa ife, ndi kutikhazikitsa ife mu Mpingo, Iye amaika mpatso ndi zinthu mu Mpingo, kuti zizigwiritsa ntchito Umunthu Wake. Ngati Mulungu ali Mulungu wopandamalire uyo, ndiye Iye amachiza odwala. Iye akhoza

kudzutsa okufa. Iye akhoza kuyeretsa akhate, kumupangitsa wakhungu kuti apenye. Iye akhoza kupereka masomphenya. Iye akhoza kuchita mitundu yonse ya zinthu izi, kumagwira ntchito mu Mpingo Wake, chifukwa ndi Mulungu mwa inu. Ndi umenewo Mpingowo.

²⁰⁸ Kodi mpingo umenewo umakhala bwanji Mpingo, pa kuwujowina Iwo? Ayi, bwana. Pa kugwirana chanza? Ayi, bwana. Mwa ubatizo wa madzi? Ayi, bwana. Mwa umembala? Ayi, bwana. Inu mumaupenza chotani Iwo? “Pakuti mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwira mu Thupi limodzi.” Ndi zimenezotu.

²⁰⁹ Aroma 8:1.

Palibe chotero tsopano kutsutsidwa . . .

“Palibe kutsutsidwa kwa chidziko.” Iwo sangakutsutseni inu za chirichonse.

Pali . . . popanda kutsutsidwa kwa iwo omwe ali mwa Khristu Yesu, omwe amayenda osati momvera thupi, koma momvera Mzimu.

²¹⁰ Ndi izo inu. Umo ndi momwe mungaweruzire Chikhristu chanu. Umo ndi momwe inu mungadziwire kuti inu mwalowa mu Mpumulo umenewo, dziko silimakuvutitsani inu aponso. Ndithudi. Inu mumaliwona ilo, mumayenda nkuchoka kwa ilo. Inu muli ndi zinazake zabwinopo zoti muziziganizira. Ndi inu apo, “Palibe kutsutsika.” Umo ndi momwe ife timalowera mu Thupilo.

²¹¹ Ndipo ndinu wotetezeka, “Kwanthawizonse.” Baibulo linanena chomwecho. Yang’anani cha uku mu Ahebri, mutu wa 10. Iye anati:

Pakuti pamene kuli zopereka za ng’ombe ndi nsembe, chikumbutso chinali kupangidwa kwa tchimo chaka chirichonse.

Koma munthu uyu, . . . kupyolera mu nsembe imodzi . . .

Lodala likhale Dzina Lake loyera!

Pakuti ndi nsembe imodzi iye wawapangitsa ungwiro kwa nthawizonse . . .

²¹² Aleluya! Osati kwa chitsitsimutso chotsatira, koma *kwanthawizonse*. “Zinthu zakale zapita; ndipo zinthu zonse zakhala zatsopano.” Ife tikuyenda mu Kuwala, Kuwala kokongola. Mbalame zikuimba mosiyana.

²¹³ Atakhala apa, ndikuyang’ana pa chidakhwa wamng’ono uyu, pafupi zaka zisanu zapitazo, ine ndikulingalira. Rosella, mleme wa maso otchingika, akuyenda mu misewu ya Chicago, ataledzera, akudzipotokola, akuyenda mu mtundu uliwonse wa tchimo lomwe linalipo, ataledzera ndi chirichonse chomwe

iyе akanakhoza kutero nacho. Ndipo usiku umodzi, Mzimu Woyera, womwe uli wachangu ndi wakuthwa kwambiri kuposa lupanga lakuthwa konsekonse, unati, “Mkaziwe, iwe ndi chidakhwa.” Aleluya! Ngati uyo si Mulungu yemweyo amene anali mmbuyomo kutaliko, yemwe anamudziwa Sara akuseka kumbuyo kwa Iye, ine sindikudziwa chomwe Iye ali.

²¹⁴ Apo mwa omvetsera kwa mkazi wina wamng’ono. Iye anapita ndipo anakamupeza iye, ndipo anamubweretsa kumeneko. Anati, “Ndiwe wachibaba cha zozunguza.” Momwe Iye amadziwira maganizo a mmalingaliro!

²¹⁵ Ndipo alaliki aakulu opezabwino atakhala apo, omwe ali ndi ulaliki wa mdziko lapansi lonse, manja awo atawapindira mmbuyo, atavala matisheti, ankaganiza kuti ife sitinkawadziwa iwo, ngati kuti iwo angakhale pa msonkhamo monga chomwecho ndipo Mulungu sakanakhoza kuwulula yemwe iwo anali. Atakhala apo, akuwoneka mosiyana, ngati iwo anali winawakenso. Mzimu Woyera unadziwa yemwe iwo anali. Ndipo iwo anakhala pamenepo, mu mitima yawo, ankaganiza kuti Izo zinali kuwerenga maganizo. Asakudziwa nkomwe za Mulungu kuposa momwe Akafula ankadziwira za walupanga waku Igupto. Ndiko kulondola. Iwo amadziwa Izo mwa lemba, koma osati mwa Mzimu. “Lemba limapha, koma Mzimu umapereka Moyo.” Ndi zimenezo. Ndilo lingalirolo. “Achangu, amphamvu kwambiri kuposa lupanga lakuthwa konsekonse, ozindikira maganizo a mu mtima.”

²¹⁶ Mvetserani. Penyani.

Ngakhalenso kuti palibe cholengedwa chirichonse chimene chiri chosaonekera pamaso pake: koma zinthu zonse ziri pambalambalanda ndi zotseguka patsogolo pa maso ake kwa iye. . . amene ife tiyenera kumachita naye.

Poona ndiye kuti ife tiri naye wansembe wamkulu. . . (Mvetserani tsopano; kwa odwala.) . . . yemwe anapita nakalowa mmiyamba, Yesu Mwana wa Mulungu, tiyeni ife tigwiritse chivomerezo chathu.

²¹⁷ “Tigwiritse molimba,” izi sizikutanthauza kumangopitirira kuchitira umboni. Ngati inu simukukhala moyowo, inu simukugwiritsa izo molimba; inu mukukhala moyo wa chinthu chachinyengo. Ndinu. . . Inu kulibwino mungokhala kunja ndi kumangoti ndinu wochimwa ndi kuiwala za izo. Musamadzinenere kuti ndinu Mkristu, nkumakhala moyo wa chinachakenso; ndinu chophunthwitsa chachikulu chomwe dziko linayamba lakhalapo nacho. Ngati muli ochimwa, vomerezani izo ndipo, zipitirirani nazo, kayanjaneni ndi Mulungu. Ngati muli Mkristu, gwiritsani molimba chivomerezo chanu, zikhalani pomwepo.

218 Penyani izi tsopano. Ine ndikufuna kuti nditengeremo izi basi ife tisanachoke.

Pakuti ife tiribe wansembe wamkulu yemwe sangakhoze kukhudzidwa ndi kumverera kwa zifooko zathu; koma mu nsonga zonse anayesedwa monga . . . ife tiri, komabe popanda kuchimwapo.

Tamverani.

Tiyeni ife chotero tibwere molimbamtima ku mpandowachifumu wa chisomo, kuti ife tikakhoze kulandira chifundo, ndi kupeza chisomo ndi thandizo mu nthawi ya chosowa.

Lodala likhale Dzina la Mulungu!

219 Tamverani, Abaptisti, Achipresbateria, Achilutera. Inu muti mundifunse ine funso ili, “Abrahamu anakhulupirira Mulungu, ndipo kunawerengedwa kwa iye kukhala chirungamo.” Ine ndikudziwa. Ndiko komwe inu nthawizonse mumapita. Izo nzoona. “Ndi chianinso chomwe munthu angachite kupatula kukhulupirira Mulungu?” Izo ndi kulondola ndendende. Izo ndi zonse zomwe iye angakhoze kuchita. Koma pamene Mulungu achizindikira chikhulupiriro chimenecho, Iye amakupatsani inu Mzimu Woyera.

220 “Tsopano kodi ine ndichite chiani, M’bale Branham? Kodi ine ndifuule?” Si zofunikira. “Kodi ine ndiyankhule ndi malirime?” Si zofunikira. Iwe ukhoza kufuula ndi kumayankhula ndi malirime, zonsezo, ndi kumakhalabe monga—monga wachikunja, ndi kumasilirabe akazi. Iwe ukhoza kumasutabe ndi kumwa, ndi china chirichonse. Ine ndawawonapo anthu akuyankhula ndi malirime, ndi kupita kunja uko ndi kukakoka ena a akatangale okhota auye kwambiri, omwe ine ndinayamba ndawawonapo. Ine ndawawonapo iwo akufuula, ndi kulira misonzi ya ng’ona, ndipo nkumakhoza kuba chirichonse chomwe iwe ungachigwire. Ine ndawawonapo iwo akukayenda, ndipo msungwana aliyense angamapite uko pa msewu, kumutembenukira. A-nha. Icho ndi chizindikiro chimodzi chabwino choti inu mulibe Iwo. Uko nkulondola.

221 Koma, m’bale, pamene inu mwadutsa kuchokera ku imfa kupita ku Moyo, zinthu zonsezo zimakhala zakufa, ndipo ndinu cholengedwa chatsopano mwa Khristu Yesu. Ngati inu muwona chinachake chalakwika, inu mumachipempherera icho, “Mulungu akhale wachifundo.” Ndipo ngati inu muwona mavuto, mmalo moti mupite kumakazilengeza, ndi kuyesera kuzipangitsa izo kuziyipira, inu muyesere kupita kwa munthuyo ndi kukazikonza izo, ndi kukazitonholetsa izo mwamsanga kumene. Uwo ndiwo Mzimu wa Mulungu mwa inu.

222 Ngati inu mupanga cholakwitsa? Inu muli ogonjera kwa icho. Ngati inu mulakwitsa, inu mukazikonza izo mwamsanga

kumene. “Musati muzilola dzuwa kukalowa muli pa mkwiyo wanu.” Ndi momwe inu mungadziwire kuti inu mwadutsa kuchokera ku imfa mwapita ku Moyo, inu mumakhala ndi chikondi, mtendere, chimwemwe, kupirira, ubwino, kufatsa, kuleza. Ife tiri naye Wansembe Wamkulu ali Kumwamba, wokonzeka kuti atiyimire pakati pa kuvomereza kwathuko. Ndi chiani icho? Ndi pamene Yesu anabwerera ku Logos, Lawi la Moto lomwe linkawatsogolera ana a Israeli, atakhala mu Kukhalapo kwa akasupe, aakulu awo, utawaleza wa Kuwala womwe unatulukirame, Mizimu isanu ndi iwiri yangwiro, Mzimu wangwiro wa chikondi.

²²³ Tsopano penyani. Choyamba ndi chikondi *changwiro*, ndicho chikondi cha Mulungu, changwiro ndi chosaipitsidwa. Chotsatira, chikubwerapo apo, ndi chikondi cha *phileo*, ndicho chikondi chomwe inu mumakhala nacho kwa akazi anu ndi ana anu. Chotsatira, chimatsika kuchokera apo, ndi chikondi *chosilira*. Chotsatira ndi chikondi *chopandaumulungu*. Ndipo icho chimangopitirirabe pansi mpaka ndi *nyansi*, chimangopitirirabe kuyipira, yipira.

²²⁴ Ndipo chirichonse chomwe chinali ndi chiyambi, chiri ndi mapeto. Ndipo zonse izo zidzachotsedwa kumene, ndi kusakhalapo chikumbutso chake, konse, ndi kubwerera kumene ku changwiro, tsiku lina. Ndipo njira yokha. . .Iwe sungaime mmusimu apa, theka la ulendo, ndi kufika pamwamba *apa*. Iwe uyenera kukhala mwa njira yonse mkati, kudalira, kupuma mwamphumphu mu chipulumutso chimene Yesu Khristu anapereka kwa iwe, mwa chikhulupiro.

²²⁵ Pali Mzimu wakuonaa umene umabwera kuchokera kwa Mulungu. Uwo ndi kasupe, kasupe wa Mulungu. Uko ndi kuonamtima. Chotsatira ndi munthu amene angachite “ntchito zabwino” kwa woyandikana naye. Chotsatira ndi munthuyo, “inu mumayenera kumuyang’anitsitsa iye.” Chotsatira ndi munthuyo, “ndi wakuba.” Chotsatira ndi munthuyo, “ndi wakupha,” woyimitsa anthu. Mukuona momwe izo zimapotokera, mpaka pansi? Koma zinthu zonse izo zimayangkhula za chenicheni.

²²⁶ Ndi chimene ine ndikunena. Nthawi iliyonse yomwe inu mumuwona munthu yemwe. . .Inu muliwone banja laling’ono likuyenda pansi mu msewu, amitima yokoma, mwinamwake ali usinkhu wa zaka makumi asanu ndi atatu. Izo zimangoyankhula kuti Kumwamba kuli banja laling’ono lomwe likuwaimirira iwo, Kumwamba. “Ngati msasa wa pansi pano usungunuka, ife tiri nawo wina Kumeneko.”

²²⁷ Ngati inu mumuwona munthu yemwe amanama, kuba, bodza, ingokumbukirani, gawo lake likumuyembekeza ku gehena, kwa iye, malo ake komwe iye ati akazunzidwe mu Kukhalapo kwa Mulungu ndi Angelo oyera, ali ndi

moto ndi miyala ya surfule. Iye adzakazunzidwa kumeneko. Osati kwanthawizonse, iye sangakhoze kukazunzidwa kwanthwizonse, nthawizonse samatanthauza konse, kwa nthawi zonse. Muyaya ndiye nthawizonse, Muyaya ndi... ulibe chiyambi kapena mapeto. Koma *kwanthawizonse* ndi “danga la nthawi.” Baibulo limati, “Kwanthawi ndi,” cholumukizira, “nthawi.” Yona anati iye anali mu mimba ya nsomba “kwanthawizonse.” Ilo ndi danga la nthawi.

²²⁸ Koma, onani, pali Moyo Wamuyaya umodzi wokha, ndipo uwo ndi Mulungu. Ndipo ngati inu muti mudzazunzidwe kwanthawizonse, ndi kusakhoza kufa, inu muli nawo Moyo Wamuyaya. Inu simungakhoze kuzunzidwa kwanthawizonse... Inu mukhoza kudzazunzidwa kwa zaka mamiloni zana, mu Kukhalapo kwa Mulungu ndi Angelo oyera, ndi moto ndi miyala ya surfule. Ine sindikudziwa kuti zinaikidwa motalika chotani. Koma potsiriza izo ziyenera kudzabwera pamapeto chifukwa izo zinali ndi chiyambi. Ndi Mulungu yekha ali nawo Moyo Wamuyaya. “Iye amene amva Mawu Anga, ndi kukhulupirira pa Iye yemwe anandituma Ine,” samakhala ndi moyo wa *nthawizonse*, “iye ali nawo Moyo Wamuyaya.” Moyo uwo womwe unayamba, osati china motsatira *apa*. Koma njira yonse mpaka Apo, Moyo Wamuyaya, *Zoe*, Moyo wa Mulungu Womwe umabwera pansu ndi kudzakhala mwa munthu, ndipo iye amakhala Wamuyaya ndi Mulungu, ndipo sangakhoze kufa. Ndi chimene Mawu amanena.

²²⁹ Tangoganizani za izo. Kodi pali Miyoyo ya Muyaya iwiri? Inu simukanakhoza kuyankha zimenezo, mukanatero inu? Pali Moyo Wamuyaya umodzi, ndipo uwo ndi Moyo wa Mulungu. Mtundu wina uwo wa moyo, ziribe kanthu chomwe iwo uli, iwo uli ndi mapeto kwa iwo. Ndipo chirichonse chomwe chinali ndi chiyambi chiri ndi mapeto. Koma chirichonse chomwe chinalibe chiyambi chiribe mapeto. Ndipo Mulungu anati Iye akanadzatiipatsa ife Moyo Wamuyaya, wopanda chiyambi, ife tinangopangidwa kukhala gawo la Iye. Ndipo kwenikweni Moyo umene uli mwa ife, sunabweretsedwe umu ndi chibadwa cha umunthu. Chibadwa chimatipatsa ife mzimu, koma mzimu umenewo unafa, ndipo ife tiri ndi Mzimu wa Mulungu. Ulemerero kwa Mulungu!

²³⁰ Kodi Mulungu anali munthu? Ndithudi. “Tiyeni ife tipange munthu mu chifanizo chathu chomwe.” Kodi Mulungu anali chiani? Fiofane, thupi. Ndipo apo munthu anapangidwa monga chomwecho ndipo anaikidwa mmunda. Koma panalibe munthu woti azilima mu nthaka, mu zokhudzira. Ndiye Iye analenga munthu kuchokera mu fumbi la dziko lapansi, mu moyo wa chinyama, ndipo munthu ameneyo ankalima nthaka. Ndipo munthuyo anagwa, pa kulakwa. Kulondola. Ndipo Mulungu, fiofane, anabwera pansu ndipo anapangidwa thupi ndipo anakhala pakati pathu, kuti amuwombole munthuyo.

²³¹ Kotero palibe chimene inu mukanakhoza kuchita. Ndinu wochimwa, pa kuyamba pomwe. Inu munawumbidwa mu kusaeruzika. Inu munabadwa mu tchimo, munabwera ku dziko kumayankhula zabodza. Inu munabadwa kuno mu dziko lino mwa chikhumbo chakugonana cha abambo anu ndi amanu. Ndipo inu ndi basi wopita ku hade monga inu mungakhalire, ine sindikusamala zomwe inu mungachite. Inu mukhoza kusamanama konse, kuba; kusunga lamulo lililonse, ndi china chirichonse; ndipo inu mudzapita ku gehena, monga mtemankhuni ku bokosi lake. Koma njira yokha yomwe inu mungakhalire konse ndi moyo kachiwiri, ndi kulandira Mzimu Woyera, Moyo Wamuyaya wa Mulungu.

²³² Nchiani chinakupangani inu chimene inu muli? Pa chiyambi, pamene Mzimu Woyera unkafungatira pa dziko lapansi, uko kunalibe kanthu koma kukhavuka kwa ziphala zamoto. Duwa laling'ono la Isitara linatulukira. Mulungu anati, "Izo zikuwoneka zokongola. Zingopitirira kufungatira." Maluwa anatulukira. Udzu unatulukira. Mitengo inatulukira. Mbalame zinawuluka kuchokera mu fumbi. Zinyama zimatulukira. Munthu anatulukira.

²³³ Tsopano, kodi izo zinachitika motani? Mwa kufungatira kwa Mzimu Woyera, kubweretsa zipangizo izi palimodzi, potashi, kashiamu; kupanga maluwa, kupanga zinyama, kukupangani inu.

²³⁴ Ndipo tsopano, inu muli nako kudzisankhira kwanokha. Mulungu akufungatiranso kwa inu, nkuti, "Ukulimva Liwu Langa? Usaumitse mtima wako, monga mu masiku a kupalamula." Apa Iye anabwera pansu, akulalikira Mawu.

"Uthenga unalalikidwa kwa iwo sunali...analibe chikhulupiriro mwa Iwo, kotero Iwo sunawachitire iwo ubwino uliwonse." Iwo anawumva Iwo, koma iwo sanawukhulupirire Iwo.

²³⁵ Mulungu anabwera pansu. Iye anawawonetsa iwo Lawi la Moto. Anawonetsa mwa aneneri Ake, zizindikiro ndi zodabwitsa, Iye anali ndi iye. Iwo sanawakhulupirire Iwo. O, iwo anakonda kuwona zozizwitsazo. Iwo anakonda kumumva mneneri. Koma kufika pa kuwakhulupirira Iwo, iwo sanatero. Miyoyo yawo imatsimikizira kuti iwo sanatero.

²³⁶ "Tsopano," Iye anati, "inu musatsatire chitsanzo icho chomwe cha kusakhulupirira." Pakuti mu tsiku lotsiriza lino, kwa mpingo wa Amitundu, Mulungu wawonekera kachiwiri; chizindikiro chomwecho, chodabwitsa chomwecho, Lawi la Moto lomwelo, likuvomerezedwa, kutsimikiziridwa. Tiyeni ife tisaumitse mitima yathu ndi kugwa mu yesero ilo lammbuyo kutaliko, la kusakhulupirira, pakuti ife tidzavundira pa dziko lapansi ndipo izo zidzakhala zonse zake.

²³⁷ Ndipo pamene Mzimu Woyera ukugogoda pa mtima wanu, [M'bale Branham agogoda pa guwa—Mkonzi.] “Patapita nthawi yaitali chomwechi, pamene inu mumva Liwu Langa, musaumitse mtima wanu.” Akuti, “Mwana Wanga, ichi ndi Choonadi.” Usati uziyang’ana pa mtumiki. Zimvetsera ku Uthengawo. Ukhulupirire Iwo. “Usaumitse mtima wako, monga mu masiku a kupalamula.”

²³⁸ Pamene iye amva “Liwu Lanu,” musaumitse mtima wanu. Ndiye inu muziti, “Inde, Ambuye, ine ndikukhulupirira.” Ndiye inu muzilowa mu Moyo, Mzimu Woyera umabwera mwa inu. Mzimu wanu wakale umafapo, umene unakupangitsani inu kusilira ndi kuda, ndi nkharwe ndi udani, n—ndi kudana ndi zinthu zonse izo, zimafapo. Ndipo inu mumakhala odzaza ndi chikondi, chimwemwe, mtendere, kupumula. Ziribe kanthu momwe mphepo zikuwombera, zonse ziri bwino.

Nangula wanga wagwira mkati mwa
chotchinga.

Kudutsa mu mphepo yokwera iliyonse ndi
yamkuntho,

Nangula wanga wagwira mkati mwa
chotchinga.

Pakuti pa Khristu, Thanthwe lolimba, ine
ndaïma;

Maziko ena onse ndi mchenga wotitimira.

²³⁹ Ndi inu apo. Eddie Pruitt, momwe iye analemba nyimbo yotchuka iyo. “Maziko ena onse,” zipembedzo zonse, tizikhulupiriro tonse, ziphunzitsa zonse, zidzazimirira kutali. Khristu!

Inu mukuti, “Chabwino, ine ndimalidziwa Baibulo.” Inu simumakhala ndi Moyo polidziwa Baibulo.

“Ine ndimamudziwa katekisimu wanga.” Iwe sumakhala ndi Moyo pakumudziwa katekisimu wanu.

“Chabwino, ndine Mkhristu.” Iwe simukhala nawo Moyo podzinenera Chikhristu.

²⁴⁰ Iwe umakhala nawo Moyo pakumudziwa Iye. Kumudziwa Iye, iwe umakhala ndi Moyo. “Ndiye inu mumalowa mu Mpumulo Wake. Inu mumatha ku ntchito zanu, monga Mulungu anachitira ku Zake.” Inu mumapangidwa kukhala Mwana wa Mulungu, wochita nawo za Mulungu. Ndipo ngati uwo—ngati Mzimu Woyera uwo ukopa kwa iwe, ndipo iwe umaukopa mobwezera nkuti, “Inde, Ambuye,” kapena kuitana.

²⁴¹ Kuitana, “Bwerani kwa Ine, nonse inu omwe mukuvutikira ndipo mwalemedwa kwambiri. Ine ndikupatsani inu Mpumulo.”

²⁴² Ndipo inu mukuti, “Aha, ndine wamng’ono. Ine ndiri. . . O, abusa anga samatero. . . Zonse zomwe ine ndiyenera kuzichita. . .” Mukuona? Inu simudzawupeza konse Iwo.

243 Koma pamene inu muti, “Inde, Mbuye wanga. Ine ndikulimva Liwu Lanu. Ine sindikuwumitsa mtima wanga. Ine sindikusamala, Ambuye, Awo ndi Mawu anu ndipo ine ndikukukhulupirirani Inu. Nditengeni ine Yesu. ’Momwe ine ndiririmu, popanda chidandaulo chimodzi, koma kuti Magazi Anga anakhetsedwera kwa ine. Ndipo apo ine ndikulonjeza, “Ine ndikukhulupirira.” O Mwanawankhosa wa Mulungu, ine ndikubwera.” Ikani manja anu pa mutu Wake wakufa, kuti, “Ambuye, ndine wochimwa, ndipo Inu munandiitana ine.”

244 “Onse omwe Atate anandipatsa Ine adzadza kwa Ine, ndipo ine ndidzamuukitsa iye pa masiku otsiriza.”

245 “Inde, Ambuye, ine ndikubwera. Ine sindikuwumitsa mtima wanga, monga iwo anachitira mwa kupalamula, ine moonadi ndikumukhulupirira Iye.”

246 Ndiye kodi Iye amachita chiani? Iye amakupatsani inu Moyo Wake, *Zoe*, Moyo Wamuyaya. Ndipo ngati Mulungu akanakhoza kutidzutsa ife kuchokera ku fumbi la padziko lapansi, komwe ife tinachokera . . . Kodi ife tinachokera ku fumbi? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Chirichonse chomwe inu mukuchiwona, chinachokera ku fumbi. Ndipo ngati Mulungu angandipange ine chimene ine ndiri lero, popanda kukhala ndi kusankha kulikonse; basi chifukwa kukhumba Kwake kunali koti andipange ine, ndi kundipatsa ine mwayi woti ndiyang’anizane nayo Kalvare ndi kupanga kudzisankhira kwanga; ndipo ine ndinapanga kudzisankhira kwanga ndipo ndinakhulupirira pa Iye; ndi mochuluka bwanji momwe Iye ati adzandiukitsire ine! Ngati Iye anandipanga ine chimene ine ndiri, popanda kusankha, ndiye ine ndinatenga kusankhako ndi kumutengera Iye mkatimu; pamene Iye anaika manja ake pa Iyemwini, ndipo analumbira pa Iyemwini, kuti Iye akanati adzandiukitse ine mu tsiku lotsiriza. Ine ndikupuma motsimikiza.

247 Ine ndiri nawo Mpumulo, osati chifukwa ine ndimapembedza Lamlungu, osati chifukwa ine ndimapembedza lasabata. Izo ziribe kanthu kochita ndi izo. Ine ndimapembedza chifukwa ine ndalowa mu mtendere Wake ndi Mpumulo: mtendere, mpumulo, chikondi, chisangalalo. Siyani mikuntho iziwuluka. Nangula wanga wagwira.

248 Kodi inu muli nacho chokuchitikirani icho, usikuuno, mzanga wa ine yemwe mwakhala muno mu kachisi wotentha uyu? Inu simunabwere kuti mudzandimvere ine. Ayi. Inu munabwera kuti mudzamve Mawu. Mvetsera, bwezi langa.

249 Tsopano ngati inu mulibe Mpumulo umenewo, inu mukhoza kuwupeza Iwo pakali pano. Inu simukusowa kuti mubwere pano pa guwa. Khalani apo pomwe inu mulipo. Khalani owona mtima, nkuti, “Khristu, ingoyankhulani kwa mtima wanga. Ine ndikudziwa kukutentha. Ndiri—ine ndangochita yense thukuta, kholophethe. Ine ndiri moyipa. Koma, Ambuye, moonu, ine

ndikhoza kumachita thukuta ndi ululu, moyipa kuposa izi, usanafike mmawa.”

Ndipo adotolo akhoza kugwedeza mutu wawo, nkuti, “Ndi vuto la mtima. Iye wapita.” Ndiye bwanji?

²⁵⁰ Bwanji ndiye? Pamene Bukhu lalikulu liri lotsegula, bwanji ndiye? Inu munaimva nyimbo imeneyo, *Bwanji Ndiye?* “Pamene iwo omwe akuwukana Uthenga, ati adzafunsidwe kuti apereke chifukwa chake, bwanji ndiye?” Bwanji ndiye? Ziganizani za izo tsopano, mwakuya kwenikweni.

²⁵¹ Pamene ife tikuweramitsa mutu wathu, ziganizani za izo.

Pamene amene akukana Uthengawu usikuuno,
Adzafunsidwa chifukwa, bwanjino?
Bwanjino? Bwanjino?
Bukhu lalikulu atatsegula, bwanjino?
Omwe ali kukana Uthengawu usikuuno,
Mudzafunsidwa chifukwa, bwanjino?

²⁵² Atate Akumwamba, izi ziri zonse mmanja Anu tsopano. Pano pali Sabata yooni ili patsogolo pa anthu. Pano pali mngelo wa Mulungu, kwa zaka zingapo zathazi, wazifuulira kuzungulira dziko. Otsutsa ndi china chirichonse ayesera kuzitsutsa Izo. Koma, nthawi iliyonse, Inu mwadzitsimikizira Nokha kuti ndinu Mulungu.

²⁵³ Dziko la sayansi, dziko la mpingo; kodi iwo ali akhungu, Ambuye? Mwinamwake muli mmodzi muno usikuuno angafune kuti alandire kupenya kwawo, kuti aziyenda mopitirira, ndi kusamuyesa Mulungu, monga mu masiku a kupalamula; osati kuyesera kuti amuyese Iye, pokhala abwino Lamlungu, kapena kusunga tsiku linalake, kapena ku kachikhulupiriro kena kake, kapena kukhala wa mu mpingo winawake. Koma akufuna kuti atulukire poyera ndi kukhala odulidwa, mu mtima, ndi kulandira Mzimu Woyera. Ndipo iwo akumufuna Iye. Mwa chikhulupiriro tsopano, iwo akuyesera kuti amulandire Iye mu mtima mwawo. Iwo akuyesera kuti apeze chisomo ndi Inu, Ambuye.

²⁵⁴ O, iwo mwina anayankhulapo mu malirime. Iwo mwina anafuulapo. Iwo akadali ndi kupsyamtima kwakale komwe kuja. Iwo akadali ndi nkhwidzi yakale yomwe ija. Iwo akadali kujeda ndi kuyankhula, ndi kuchita zinthu zomwe iwo samayenera kumachita. Iwo sakuzifuna izo, Ambuye. Bwanji ndiye, pamene Bukhu lalikulu ilo liti lidzatsegulidwe? “Koma,” anati, “oterowo sadzalowa mu Ufumu.” “Khalani inu chotero angwiro, ngakhale monga Atate anu Kumwamba ali angwiro.” Chirichonse chopewera sichidzalowa umo. Kodi iwo akudalira mwathunthu, usikuuno, mwa wopachikidwayo? Ngati sichoncho, Ambuye, mulole iwo angopanga “inde” mmodzi Wamuyaya uyo pakali pano.

255 Kuti, “Ambuye, I..Palibe kutengeka, koma ine ndikungomverera Chinachake pansu mu mtima mwanga, pali Chinachake chikundiiza ine, ‘Ine ndikhoza kuzichita izo pakali pano, mwa chisomo Chanu.’ Ndipo ine tsopano ndikukuvomerezani Inu ngati Mpulumutsi wanga wanga. I—ine ndikukana zinthu zonse za mdziko, ndipo ine ndikufuna kuti ndilowe mu Mpumulo wanu. Ndipo ine ndikukhulupirira ine ndikuchita izo pakali pano. Ine ndikukhulupirira Mzimu Woyera ukundibweretsa ine mu malo awo omwe.”

256 Pamene mutu uliwonse uli woweramira. Kodi winawake akumverera mwanjira imeneyo pakali pano? Kwezani dzanja lanu, “Mzimu Woyera tsopano ukundibweretsa ine mu malo pomwe ine sindingamajede kenanso.” Mulungu akudalitsemi inu. “Ine sindimachita zinthuzo. Mkwiyu wanga wapita. Ine ndikhoza kumakhala mu mtendere ndi chisangalalo ndi kupirira, kuyambira pakali pano. Ine ndikukhulupirira Mulungu akuyankhula kwa ine pakali pano, kuti ine ndikhoza kuzichita izo kuyambira ora lino mpakana, mwa chisomo Chake.” Kodi inu mungakweze manja anu? Mulungu akudalitsemi inu. Mulungu amudalitse dona wamng’ono. Winawakenso? “Ine tsopano ndikukhulupirira.”

257 Musamuyese Iye, monga mu tsiku la kupalamula. Musati muziganiza kuti chifukwa ife timapita ku tchalitchi Lamlungu, kapena timasunga sabata. Paulo anati, “Inu amene mumasunga masiku kapena kuoneka kwa mwezi, kapena zina zotero, ine ndikukuopani inu. Lamulo pokhala nawo mthunzi wa zinthu zabwino zakudza, ndipo osati fano lomwe la chinthucho, silingamupange wopembedza kukhala wangwiro.” Koma Khristu amakupangani inu kukhala wangwiro, wangwiro pamaso pa Mulungu. Iye amachotsapo tchimo lanu, amachotsa kutsutsidwa kwa inu, amakupatsani inu chikondi Chake ndi chisangalalo.

258 Kodi inu mungalowe mu Mpumulo tsopano? Winawakenso akweze dzanja lake, nkuti, “Ine ndachita zimenezo.” Mulungu akudalitsemi iwe, dona wamng’ono, cha kuno kumanzere kwanga. Mulungu amudalitsemi mwamuna yemwe wakhala cha kumanja kwanga. Kulowa mu Mpumulo Wake, ziganizani za izo basi tsopano.

259 Zipempherani, “Basi momwe ine ndiriri, Ambuye, popanda kudzikanira kumodzi; ine sindine wabwino. Palibe chomwe ine ndingakupatseni Inu, koma moyo wanga wokha wakale, wotopa, wamachimo. Kodi Inu mungandilandire ine? Kunditsuka? Mundipepuza? Chifukwa, ine ndalonjeza kuti ine ndizikhulupirira. O Mwanawankhosa wa Mulungu, ine ndikubwera. Ine tsopano ndikubwera, ndikukhulupirira kuti tsopano ine ndadutsa kuchokera ku imfa kupita ku Moyo. Chifukwa, pomwe pano pa mpando wanga, ine ndakuvomerani

Inu ngati Mpulumutsi wanga ndipo ine ndikumverera mtendere mu mtima mwanga.”

²⁶⁰ Asanu akweza manja awo mmwamba. Angatero mmodzi wina, yemwe akumverera mwanjira imeneyo, kwezani dzanja lanu? Ngati sindinu Mkhrstu, muvomereni Iye pakali pano.

²⁶¹ Ngati inu mukudzinenera kuti ndinu Mkhrstu ndipo simunayambe mwakhala mwa mtundu umenewo, inu mukanali wochimwa, ziribe kanthu moyo inu—zomwe inu mwachita, kapena momwe inu mukuyesera kudzipanga nokha. Zomwe inu muchita si zovomerezedwa. Ndi zomwe Iye anachita. Chilungamo chanu chomwe sichiti chilindiridwe. Ngati inu musiya kusuta basi chifukwa inu munati, “Chabwino, ine ndibwino ndisiye kusuta chifukwa ine ndikudzinenera Chikhrstu.” Mulungu samavomereza izo. Ngati inu musiya kusilira akazi, basi chifukwa chakuti inu mukudzipangitsa nokha kuti muzichita izo, Mulungu samavomereza zimenezo. Icho ndi chinachake chimene inu mukuchita. Izo ndi ntchito. Ndi chisomo chimene chimakupulumutsani inu. Kodi Mulungu wabwera kwa inu ndi kuchichotsa chinthu chonsecho mwa inu? Ndicho chinthu chotsatira.

²⁶² Inu mukuti, “Ine ndajowina mpingo, ndipo chotero ine ndikuyenera kusiya zinthu izi.” Mulungu sanazivomereze izo, si chimene inu mungati mupereka. Iye amangovomereza chimene Khristu apereka. Iye amakupatsani inu Moyo Wamuyaya, ndi kuchotsa izo kwa inu. Kodi inu muwulandira Iwo?

. . . pa nyanja, yanamondwe,
Bwera, zikikatu mu Mpumulo wa moyo,
Nena, “Wokonedwa ndi wanga.”
Ndazika moyo wanga . . .

Chabwino, inu mukhoza kukweza dzanja lanu. Uthenga watha tsopano. Tiyeni tizingopembedza tsopano.

Sindzayenda mu nyanja yowopsya;
Namondwe angawopsye pansi, pansipo,
Mwa Yesu ndatetezeka.

²⁶³ Aliyense tsopano, mwa kupembedza.

Ndazika moyo mu Mpumulo wammwamba,
(Sabata)
Sindidzayendanso mu nyanja yowopsya;
Namondwe angawopsye, pansi pansipo,
Mwa Yesu ndatetezeka.
Mndiwalire, . . .

Ingodzimasulani nokha. Tsekani maso anu. Mukumverera Mzimu wokoma uwo? Ndiko kupembedza. Uthenga watha. Uku ndi kupembedza.

Mu nyumba ya Kuwala mndiwalire,
Mndiwalire, Mbuye, mndiwalire,
Mu nyumba ya Kuwala mndiwalire.

²⁶⁴ Ndi angati akumverera mwabwino kwenikweni? Kwezani dzanja lanu. Mzimu wokoma, wodzichepetsa uwo, ndi Umenewo.

Mongatu Yesu, basi mongatu Yesu,
Ndifuna ndifane Naye;
Mnjira ya moyo, ku ulemerero,
Ndipempha ndifanane . . .

Zingomamupembedzani.



BUKHU LA AHEBRI

Mauthenga khumi ndi umodzi awa a M'bale William Marrion Branham, anaperekedwa mu Chingerezi kuyambira Ogasiti 21 kudutsa Seputembala 22, 1957, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., anatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nadindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2009 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org